


# MULUNGU

## AMAZINDIKIRITSIDWA

### NDI MAKHALIDWE AKE

 Atate Akumwamba, ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mwayi wotitsogolera ife kuno ku Beaumont, Texas, kachiwiri. Pamene ine ndikuyang'ana mozungulira mmakonde awa, ndikukumbukira nthawi zomwe ife tinali kuno kale, ndi zinthu zazikulu zomwe Inu munachita, sindikukaikira ambiri a anthu amenewo akhala pomwe pano usikuuno. Ngati Inu mukanati musakhudze matupi awo odwala, iwo sakanakhala pano usikuuno, koma Inu munatero, ndipo iwo ali pano. Zikumbutso zambiri zikuyenda, izo zonse zidzapita mu Muyaya ndi ife.

<sup>2</sup> Ife tikupemphera kuti Inu mutipatse ife kutsanulira kwakukululu kwa Mzimu. Mutidalitse ife palimodzi. Mudalitse mpingo uliwonse, membala aliyense.

<sup>3</sup> Ndipo, Ambuye, makamaka mudalitse m'bale wathu wamng'ono wokonedwa pano, M'bale Pearry Green, amapita kutsogolo kuti akayesere kuti afotokoze Izi. Mulole anthu a— a mzinda wokonedwa uwu awone—kukhudzidwa kumene mnyamata uyu ali nako kwa anthu kuno, kuti awabweretse iwo kwa Khristu amene iye amamukonda. Ndipo iye akuyesetsa kuti abweretsemo utumiki uliwonse umene iye angaganize kuti ungakhale wolondola, umene iye wauwunikira ndi Mawu, ndipo iye akufuna kuwona anthu akupulumutsidwa.

<sup>4</sup> Tithandizeni ife, Atate, mu kuyesetsa kwathu, pamene ife tikudzipereka tokha kwa Inu ku utumiki, kwa ulemu ndi ulemelero wa Mulungu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

<sup>5</sup> Tsopano, ife... ingokumbukirani, usiku uliwonse tsopano, muzibwera ndi winawake limodzi nanu, kapena muzifikira pa foni ndi kumuwuza winawake, ndi kumuuzza m'busa aliyense, mpingo uliwonse. Ziribe kanthu momwe zimenezo ziriri, ngakhale iwo atakhala akutsutsana ndi ife, bola ngati inu mungathe kubwera, kudzakhala pansu, kukhala ndi khalidwe ndi kukhala abwino, ife ndithudi tidzakuyamikirani inu chifukwa chodzakhala pano.

<sup>6</sup> Ndipo tsopano muzibweretsa Baibulo lanu, muzibweretsa pensulo, kumadzalemba phunzirolo. Nkumapita, kukafufuza izo, kukazifufuza izo ndi Mawu ndikukawona ngati

izo ziri zolondola kapena ayi. Mukuona? Ndiyeno osati muzitenga fioloje yanuyanu, muzingozitenga izo momwe Baibulo linalembera. Mwaona, nthawi zambiri ife tikhoza kunena kuti, “Ilo likutanthauza *izi, izi* ndi chimene Ilo likutanthauza.” Mulungu samasowa wotanthauzira aliyense, Iye amadzitanthauzira Mawu Ake Omwe. Mukuona?

<sup>7</sup> Mulungu anati, “Kukhale kuwala,” ndipo kuwala kunadzakhalapo. Izo sizinasowe—sizinasowe kutanthauzira kulikonse. Iye . . . Izo zinachitika basi momwe Iye ananenera. Iye anati, “Namwali adzayima,” ndipo iye anatero. Izo sizinasowe kutanthauzira kulikonse.

<sup>8</sup> Mulungu analonjeza zinthu zina za m’badwo uno zimene zikuyenera kuchitika! Iye ananena izo, izo sizikusowa kutanthauzira pamenepo. Mulungu ananena chomwecho, ndipo Iye amatanthauzira, Iyemwini, koteru Baibulo linati Iwo ndi opanda kutanthauzira kwa mseri. Mulungu amatanthauzira Mawu Ake Omwe powatsimikizira Iwo.

<sup>9</sup> Tsopano ine ndikudabwa ngati ife tingayime pamene ife tikuwerenga Mawu Ake, kuchokera mu Bukhu la Ahebri, mutu wa 1. Chifukwa chimene ine ndikukupemphani inu kuti muyime, ndi polemekeza Mawu awa. Ndimakhulupirira kuti Mawu ndi Mulungu, “Pachiyambi panali Mawu, Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anadzasantulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.” “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” umenewo ndiwo mutu wa misonkhano yathu. Choteru, pamene tikuwerenga Mwini Wake wosindikizidwa apa pa Mawu awa, ife timayima. Pamene tinalonjeza kukhulupirika ku mbendera, mbendera yathu ikamadutsa, ife timayima molemekeza mbendera yathu, fuko lathu, timayenera kuchita zimenezo. Ndiye, ndi mochuluka bwanji ife tikuyenera kuimirira pamene tikuwerenga Mawu a Mulungu! Ahebri 1:1-3, pamene ife tikuwerenga:

*Mulungu, amene mu nthawi zakale ndi m’njira zosiyanasiyana ankayankhula mu nthawi zakale kwa makolo anthu mwa aneneri,*

*M’masiku otsiriza ano wayankhula kwa ife mwa Mwana wake, amene iye wamuyika kukhala wolowa pa zinthu zonse, mwa iyenso anapanga mayiko;*

*Amene pokhala mu kuwala kwa ulemelero wake, ndi chifaniziro chofotokozedwa cha umunthu wake, ndi kunyamula zinthu zonse mwa mawu a mphamvu yake, pamene iye mwa iyemwini anayeretsa machimo athu, anakakhala ku dzanja lamanja la Ufumu kumwamba;*

<sup>10</sup> Tiyeni tipemphere. Ndi angati tsopano, ndi mitu yoweramitsidwa ndi mitima, akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero, kuti kupyolera mu msonkhano uno, panapake,

Mulungu apereke chopempha chanu? Mungokweza dzanja lanu. Ambuye akuwona dzanja lanu.

<sup>11</sup> Atate athu Akumwamba, monga momwe maso anga a umunthu akuwonera, panali unyinjira wathunthu wa manja. Ndithudi vumbulutso la M'bale Green ndi chikhumbo changa choti ndibwere, zinali zolondola. Tsopano, Atate, apatseni iwo chokhumba chawo, molingana ndi Mawu Anu ndi lonjezo Lanu. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu. Ndipo mulole miyoyo yathu ikhale yokwanirana ndi Mawu, kuti Mawu asandulike thupi pakati pathu ndipo awapatse anthu chikhulupiriro chotengera kuchokera mosungira mwawo Kumwamba, zimene Yesu anawalipirira iwo kalekale, kwa machimo awo ndi matenda, pamene iwo ali paulendo. Tidalitseni ife tsopano, ife tikupemphera, pamene ife tikuyembekezera pa Inu kuti muwululire kwa ife Mawu Anu, ndi kuwapanga Iwo kukhala thupi pakati pathu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Mukhoza kukhala pansa.

<sup>12</sup> Tsopano ine ndingatero, ngati mungayesere kutero, osayendayenda pozungulira momwe inu mungathere kuthandizira, ine ndikutanthauza kuimira ndi kumapita, mpaka basi maminiti forte-faivi, fifite otsatirawa, chinachake chonga chimenecho. Tsopano, a—str- . . .

<sup>13</sup> Chinthucho ndi ichi, ife tikufuna kuti tidziwe chimene chiri Choonadi. Ndipo ndicho Choonadi chimodzi chokha chimene ine ndikuchidziwa, ndi Baibulo. Tsopano, Mulungu adzaweruzza dziko lapansi tsiku lina, ife timakhulupirira zimenezo, ndipo aliyense wa ife achivundi tidzabweretsedwa mu Kukhalapo Kwake kuti tidzaweruzidwe. Ine ndiri ndi zolembe zingapo ndazilemba apa, ndi Malemba amene ine ndikufuna kuti ndilozerepo mmaminiti pang'ono.

<sup>14</sup> Tsopano kumbukirani, ngati ine ndingafunse usikuuno, “Kodi pali Wakatolika pano?”

“Inde,” iwo angatero. Ndipo mwinamwake . . .

“Chabwino, kodi Mulungu adzaweruzza dziko ndi chiyani?”

Iwo angati, “Ndi mpingo wa Katolika.”

<sup>15</sup> Ndiye ine ndikanayankha kuti, “Mpingo wa Katolika wake uti?” Iwo samagwirizana. Pali kusagwirizana kochulukika. Wina ndi wa Chiroma, ndipo winayo ndi Mgriki, ndi wa Orthodox, ena otero. Ife tiri nayo yochulukika. Ngati ndingatero . . .

<sup>16</sup> Amethodisti angakhoze kudzuka, nkudzati, “Iye adzaliweruzza ilo ndi mpingo wa Methodisti.” Chabwino, ngati izo ziri chomwecho, ndiye Abaptisti alibe mwayi. Ndipo ngati iwo adzaweruze ilo ndi Abaptisti, ndiye Amethodisti alibe mwayi.

17 Chifukwa, kumbukirani, kubwereza Mawu kumodzi kwapang'ono molakwitsa, kumodzi (osati onsewo, basi osati onse a ndime imodzi), kadontho kamodzi kakang'ono kokha basi ka kusakhulupirira Mawu, kanayambitsa imfa iliyonse, matenda aliwonse, chisoni chirichonse. Ameneyo anali Eva, m'munda wa Edeni. Tsopano ngati zonsezi zinabwera chifukwa cha chimenecho, chifukwa cha dona mmodzi yekha osawamvetsa Mawu...Iye—iye sanachite zimenezo mwadala, iye anali “atanyengedwa,” Baibulo linatero. “Kunyengedwa,” ndi Mawu, zinayambitsa zonsezi, ndiye inu ndi ine sitikubwerera mmbuyo ndi chirichonse chochepera kuposa Mawu onse.

18 Tsopano, ine ndikukhulupirira, Baibulo limanena kuti Iye sadzatero, ine sindimakhulupirira kuti Mulungu adzaweruzza dziko ndi mpingo wa Chipentekoste, ndi Methodisti, Baptisti, kapena Katolika. Iye adzaweruzza ilo ndi Yesu Khristu, Iye ananena chomwecho. Ndipo Khristu ndi Mawu, “Pachiyambi panali Mawu, Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu. Yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

19 Chinthu chonsecho ndi Chamuyaya chachikulu. Umuyaya sunachite kuyamba ndipo sungathe konse. Chotero, mwa Mmodzi Wamuyaya wamkulu uyu munali zikhumbo, kuti adzakhale Atate, kuti adzakhale Mwana, kuti adzakhale Mpulumutsi, kuti adzakhale Mchiritsi, ndipo zinthu zonsezi zinali mwa Iye. Ndipo chinthu chokhacho chimene chikuchitika tsopano, ndi kuwonetsera zikhumbo Zake. Ndizo zonse.

20 Tsopano, maina athu anayikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ndipo pamene Mawu akhudza icho, ngati muli kuwala kulikonse mmenemo kumene kunadzozedweratu ku Moyo, Yesu anati, “Palibe munthu angabwere kwa Ine pokhapokha Atate Anga atamukoka, ndipo onse amene Atate Anga anandipatsa Ine adzabwera kwa Ine.” Kotero, inu mukuona, ndi Mawu, mosalekeza, Mawu, Mawu.

21 Tsopano, ine ndikufuna kuti ndiyankhule usikuuno pa phunziro, lochokera mu nkhani kuchokera mu lemba ili limene ife tinawerenga, *Mulungu Amazindikiritsidwa Ndi Makhaliidwe Ake*.

22 Tsopano, pafupifupi chirichonse chimene timachipeza chikhoza kuzindikiritsidwa ndi makhaliidwe ake.

23 Tsopano, ife tikuzindikira, monga mu moyo wa zinyama, inu mutenge monga mmoyo wa mbalame. Tsopano, inu mutenge monga a—mpheta, pamene iyo ikuwuluka, ndi mbalame ya katawa, izo zimawoneka mofanana kwambiri. Koma khalidwe la mpheta, iyo imakupiza mapiko ake ndi kumatsika, ndipo kenako mmwamba ndi pansu, mmwamba ndi pansu. Limenelo ndi

khalidwe. Ngati mungazindikire, katawa amawuluka kwambiri mu mzere wa njuchi.

<sup>24</sup> Inu muwone chinziri pamene icho chikukwera mmwamba, choyera, momwe icho chimawulukira. Muwone chinziri cha Gambel pamene icho chikukwera mmwamba, asaki inu. Inu mukuona, pamakhala kusiyana. Mudzawone ya jacksnipe ndi ya Wilson snipe, khalidwelo limafotokoza chimene iyo ili.

<sup>25</sup> Nkhosa yaikulu itayima m'mphepete mwa phiri, ngati iyo ikanatembenuza nsana wake, mbali ya kumbuyo ya nsana ndi yoyera, gawo linalo ndi lotuwa. Ngati iwe sukudziwa makhalidwe a nkhosa imeneyo, iyo ikhoza kukhala mphalapala. Mukuona? Mwaona, iwe umayenera kudziwa makhalidwe a izo, kuti uzidziwa chimene chiri ndi chimene sichiri. Zinthu zambiri ife tikanakhoza kumangopitiriza kukuuzani inu zokhudza moyo wa zinyama.

<sup>26</sup> Ndiyeno ife tibwere ku moyo wa munthu, makhalidwe pakati pa mwamuna ndi mkazi. Pali kusiyana. Awiri onsewo ndi anthu, koma makhalidwe a awiriwa amawazindikiritsa iwo. Ndinali kuwerenga nthawi ina yapitayo za limodzi la mavuto amene anayikidwa ku—yesero la Solomoni, ndi mfumukazi, kuti anali ndi akazi ena ovala ngati amuna. Ndipo Solomoni anawapangitsa iwo kuyenda ndi kuchita zinthu zingapo, mwamsanga iye anati, “Amenewo ndi akazi.” Mwaona, chifukwa chakuti iye anakhoza kudziwa ndi momwe iwo ankachitira, kuti a—makhalidwe a iwowo anali akazi. Pamakhala chinachake cha izo, chimene sungathe kuchibisa, ndi—ndi mkazi chifukwa lake—khalidwe lake limamuwonetsera iye kukhala mkazi.

<sup>27</sup> Izo ziri ngati dzanja lamanja ndi lamanzere pa anthu. Iwo awiri onsewo ndi anthu. Inu muwone, ndipo mmodzi wa iwo ndi wa dzanja lamanja ndipo winayo ndi wamanzere. Muwone momwe makhalidwe awo amawazindikiritsira iwo, mutha kudziwa ngati iwo ali a dzanja la kumanja kapena kumanzere kapena ayi. Mukuona? Komabe iwo awiri onse ali ndi manja, manja awiri onse amawoneka ofanana ndendende basi, chimodzimodzi basi.

<sup>28</sup> Ine ndikhoza kugwetsera chinachake chaching'ono apa. Yesu ananena, mu Mateyu, mutu wa 24, kuti, “Mmasiku otsiriza, mizimu iwiriyo idzakhala yoyandikana kwambiri mpaka iyo ikanadzanyenga osankhidwa omwe ngati kukanakhala kotheka.”

<sup>29</sup> Tsopano, zimenezo ndi kungoyang'ana pa dzanja lamanja ndi lamanzere. Awiri onse ali ndi zala zazikulu, zala, zikhadabo, zala zazing'ono, zala zapakati, ndi zina zotero, zolozera, zonse ndi zala zosiyanasiyana. Iwo, awiri onse ali ndi zidindo, kokha kuti chimodzi chinatembenukira mbali imodzi ndi china inayo, ziwiri zonse zidindo zofanana, zopangidwa mwanjira yomweyo, zidindo za chala. Chirichonse chimawoneka mofanana, kusiyana

kokhako ndi khalidwe lake. Umodziwo ndi nkono wamanzere ndipo winawo ndi nkono wamanja, ndiko kusiyana kokhako.

<sup>30</sup> Ndipo umo ndi momwe mizimuyo idzakhalire mu tsiku lotsiriza, iyo idzatero, chikhalidwe chake chokha cha iyo chidzazindikiritsa ngati iwo uli wa Mulungu kapena ayi. Umodzi wa iyo udzakhala wolondola ndipo winawo udzakhala wolakwika, inu mudzadziwa izo mwa chikhalidwe cha Mulungu. Mwangwiro basi, izo zikuyenera kudzakhala mwanjira imeneyo. Koma dzanja lamanja, tinganene kuti “lolondola,” ndipo dzanja lamanzere linali “lolakwika,” mwaona, kapena motsemphanitsa, chimodzi cha izo. Iyo imazindikiritsidwa ndi makhalidwe awo. Mungathe kuidziwa iyo kokha ndi makhalidwe ake.

<sup>31</sup> Monga Israeli anali mu ulendo wake, akubwera kuchokera ku Igupto. Tsopano, Mulungu anali ndi Israeli, Iye anali atawawonetsa iwo chizindikiro chachikulu kumusi uko, anatumiza mneneri kwa iwo ndipo anazindikiritsa Mawu Ake olembedwa. Ndipo pamene Iye anawabweretsa iwo, ife tikuwona chikhalidwe Chake, momwe Iye anakumanirana ndi Mose, zinthu zimene Iye anachita. Ndipo pa yake. . . panjira akupita, iwo anafika ku fuko lina, limene linali Moabu. Ndipo Moabu linali fuko lalikulu, tsopano, osati achikunja, mwanjira iliyonse. Amenewo anali ana a ana aakazi a Loti, ndipo iwo anali okhulupirira. Tsopano, penyani mafuko awiriwo. Limodzi la iwo linali fuko lodziwika, enawo anali amwendamnjira chabe. Ndipo tsopano iwo anafika pa malo pamene mtundu waukulu uwu wa Moabu unayima molunjika mu mzere kumene wa njira yawo ya ntchito, yopita ku dziko lolonjzedwa. Tsopano iwo anali. . .

<sup>32</sup> Tayang’anani pa—mafuko awiriwo, lirilonse la iwo linali ndi mneneri. Mmodzi wa iwo anali mphunzitsi wamkulu ndi mneneri, Balaamu. Winayo anali Mose. Tsopano Balaamu anatsikirako akuchokera. . . kuti adzatemberere Israeli.

<sup>33</sup> Ndipo, zindikirani, onse a iwo anali mwamtheradi achikhazikitso. Mneneri, wachikhazikitso kuchokera kwa Balaamu, anati, “Mundimangire maguwa seveni,” imeneyo ndi ndendende nambala ya Mulungu. “Ndipo mupereke pa guwa lirilonse nsembe yoyera, ng’ombe yamphongo,” imene ndi ndendende nsembe yomweyo imene iwo anali nayo uko mu msasa wa Israeli. Ndipo iye anati, “Pa guwa la nsembe lirilonse mupereke nkhoa yamphongo,” kuyankhula za kudza kwa Khristu. Ndipo kumusi mu Israeli iwo ankapereka nsembe yomweyo.

<sup>34</sup> Maguwa omwewo, Mulungu yemweyo, koma limodzi la iwo linali lolakwika ndipo linalo linali lolondola. Ndipo tsopano njira yokhayo imene inu mukanadziwira limene linali. . . Pamene izo zinabwera, mwachikhazikitso, ku Mawu, awiri onse a iwo anali olondola. Koma, inu mukuona, mmodziwo, zolinga

zake zinali zolakwika, iye anali kuyesetsa kuti amudule m'bale wake pa mzere wa lonjezo limene Mulungu anamupatsa iye.

<sup>35</sup> Chinthu china, mmodziyo, mneneri wa Balaamu, anali wachikhazikitso, koma mneneri Mose ankazindikiritsidwa ndi makhalidwe a Mulungu. Apo panali Lawi la Moto, Kuwala kwauzimu kutapachikika pa iwo. Ndipo munali machiritso aakulu mu msasa wawo, Mulungu wauzimu akuwonetsera zizindikiro zauzimu. Ndipo iwo ankakhala ndendende ndi Mawu a lonjezo amene Mulungu anamupatsa Abrahamu mmbuyo mu nthawi imene mafuko onsewo ankayamba. Koma, tsopano, Mose anali ndi lonjezo la Abrahamu, akupita ku dziko lolonjezedwa. Balaamu, nayenso mneneri wa Ambuye, atayima kumusi kumeneko. Ndipo njira yokhayo imene inu mukanzindikirira, osati mwa chiphunzitso chawo chachikhazikitso, koma mwa chikhalidwe cha Mulungu.

<sup>36</sup> Kunkamveka kuwomba kwa a—kufuula kwa liwu la Mfumu kumusi kuno ndi Israeli. Chitetezero chinali chikugwira ntchito, Njoka ya Mkuwa, Thanthwe lokanthidwa. Ndipo Mulungu anali ndi iwo, akuzidzindikiritsa Yekha mu Kuwala kwauzimu, ndi kumachiritso nthenda zawo ndi matenda pamene iwo ankapitirira. Makhalidwewo ankatsimikizira chimene Iye anali, akukhala mu mzere wa Mawu a m'badwo umenewo, kwa m'badwo umene iwo ankakhalamo. Makhalidwe a Mulungu ankazidzindikiritsa Iwoeni ndi Mose. Mwaona, makhalidwe a Mulungu ankazindikiritsidwa ndi Mose. Lawi la Moto, chitetezero chikuchitapo, chauzimu, Thanthwe lokanthidwa, ndi iwo... komanso Njoka ya Mkuwa, kuyankhula za machiritso, ndiyeno—ndiye kenanso iwo anali mu mzere wa ntchito, wa lonjezo la Mulungu.

<sup>37</sup> Komanso, makhalidwe a Mulungu si achithupithupi. Khalidwe la Mulungu ndi lauzimu, chifukwa Iye ndi Mlengi. Iye ndi Wauzimu. Ndipo pamene khalidwe la Mulungu liyamba kudziwonetsera lokha, ilo limakhala losazolowereka ku maganizidwe amakono kotero kuti limawachotsa iwo pa mzere. Iwo sangakhoze kumvetisa Zimenezo, komabe Iye samachoka konse ku lonjezo Lake. Mulungu mmibadwo yonse, ine ndanenapo, ankawayika Mawu.

<sup>38</sup> Tiyeni tingotenga, mwachitsanzo, mmodzi. Kunali Yosefe, mwamuna wake wa Mariya. Ndipo tsopano iye anali atatomera dona wamng'ono uyu, ndipo iwo anali oti akwatirana. Koma kenako iwo asanabwere pamodzi, iye anapezeka ali ndi mwana wa Mzimu Woyera.

<sup>39</sup> Tsopano, ife tonse timakhulupirira zimenezo, ngati ife tiri Akhristu. Ife tikuyenera kukhulupirira zimenezo kuti tikhale Mkhristu. Limenelo ndi Baibulo. Inu mukuyenera kukhulupirira Mawu aliwonse mu Baibulo, kuti mukhale Mkhristu. Tsopano,

chifukwa ngati Mzimu Woyera uli *umu*, Iwo udzavomereza Mawu aliwonse ndi lonjezo lirilonse ndi “ameni.”

<sup>40</sup> Chifukwa, tsopano, Yosefe anali munthu wolungama, iye anali munthu wabwino. Ndipo sindikukayika kuti Mariya anali atamuza iye za kuchezero kwa Gabrieli, ndi momwe iye akanati adzaphimbidwe ndi Mzimu Woyera, ndipo anali woti adzayime ndi kubala Mwana wamwamuna, ndipo Dzina Lake linali loti adzatchedwa “Yesu,” momwe iye akuyenera kuti ananena izo kwa Yosefe. Ndipo Yosefe amakhoza kuyang’ana mmaso ake aakulu abulauni, ndipo iye amakhoza kuwona kusalakwa kwa izo, ndipo iye anafuna kuti akhulupirire zimenezo. Iye ankafuna kuti akhulupirire izo ndi mtima wake wonse, komabe izo zinali zachilendo kwambiri, ndipo iye anaganiza zomusiya iye, mwamseri.

<sup>41</sup> Tsopano, ngati munthu ali woonamtima mu izo, Mulungu adzapanga njira ina yomuwonetsera munthu ameneyo kuti icho ndi Choonadi. Iye amakhala wokakamizika, ngati iwe uli woona mtima. Ngati iwe wachiwona Icho, ndi kuchoka kwa Icho, ndiye ndiwe woti uweruzidwe. Koma, ngati iwe uli woona mtima ndipo nkuchiwona Choonadi!

Tsopano, Yosefe anango “ganizira.” Iye anati, “Izo ndizosazolowereka kwambiri!”

<sup>42</sup> Umo ndi momwe ziriri lero, kuti anthu, amuna abwino, amuna abwino, amuna amakhalidwe abwino, atumiki abwino, ambiri a iwo, ansembe ndi ena otero, ndi anthu abwino, koma kutsimikizira kwauzimu kwa lonjezo la tsiku lino ndi kosazolowereka kwambiri, iko kumawaponyera iwo kunja kwa mulingo wawo. Iko kumachita zimenezo chifukwa iko kukuwonetsera khalidwe la Mulungu.

<sup>43</sup> Tsopano, Yosefe, mwamuna wake, pokhala mwamuna wolungama, posafuna kuti amupange iye kukhala chitsanzo chapoyera. Iye sanakhulupirire izo; iye—iye anayesetsa kutero. Koma pamene iye anali kulingalira pa zinthu izi, Mngelo wa Ambuya anayankhula kwa iye ndipo anamuza iye.

<sup>44</sup> Tsopano, Iye samayenera kuti nthawizonse aziyankhula mu loto, Iye akhoza kudziwulula Yekha kwa inu mwa Mawu, ndi kukuwonetsani inu kuti Iwo owona, ngati inu muli owonamtima mokwanira kuti muyang’ane mwa Iwo ndi kuwona ngati ilo liri khalidwe la Mulungu limene likudziwonetsera lokha, koma nthawizonse mu mgwirizano uliwonse ndi Mawu olonjezedwa.

<sup>45</sup> Ndipo chinthu china, Mawu a Mulungu nthawizonse amakonza cholakwika. Inu mukukhulupirira zimenezo? Mawu amazikhazikitsa izo. Pamene Mulungu atsimikizira Mawu amenewo, iwo amakhazikitsa izo.

<sup>46</sup> Tsopano tiyeni, mmodzi yekha mmalingaliro anga amene ine ndikufuna kumuganizira. Ife sititenga nthawi yochuluka kwambiri, chifukwa ife tikufuna kupempherera odwala ena.

Tiyeni tiwone. Pamene Yesu, pokhala Mawu... Baibulo linati Iye anali Mawu. Ife tonse tikugwirizana ndi zimenezo, kuti Iye anali Mawu. Zindikirani pamene Iye anali usinkhu wa zaka thwelovu. Tsopano, ife tiribe zonena zakuti Iye ankapita ku sukulu. Koma Mnyamata wamng'ono wazaka thwelovu pafupifupi wotalika *chonchi*, iwo, makolo Ake, Mariya ndi Yosefe anapita ku kachisi ku... kumtunda ku... kukapembedza pa paskha. Ndipo pamene iwo anali kumtunda kumeneko, iwo anayamba kubwerera kwawo itatha paskha, iwo anali ndi ulendo wa masiku atatu, ndipo sanamupeze Yesu paliponsepo. Ndipo potsiriza iwo anamupeza Iye, atapita masiku atatu akumufunafuna Iye, mu kachisi, akutsutsana pa Mawu a Mulungu ndi akulu akuluwo.

<sup>47</sup> Ndipo tamvetserani kwa Mariya tsopano. Tsopano kwa anthu amene amamutenga iye kukhala mulungu wamkazi, penyani. Inu mukuona, a—mkaziyo ananyengedwa pachiyambi. Ndipo mumuwone iye apa. Ngati inu simunazindikire izo, penyani izi. Iye anati, “Atate ako ndi ine takhala tikukufuna Iwe, ndi misonzi.” Zindikirani, iye anawutsutsa umboniwo (pamaso pa ansembe amenewo) umene iye ankawunena. Iye anati iye anali ndi “pakati pa Mzimu Woyera,” ndipo apa iye anamutcha “Yosefe” bambo Ake.

<sup>48</sup> Tsopano penyani Mnyamata wa usinkhu wa zaka thwelovu zakubadwa ameneyo, pokhala Mawu a ora limenelo. Iye anali Mawu olonjezedwa a ora limenelo, Mesiya wodzozedwayo. Penyani chimene Iye ananena, “Kodi inu simukudziwa kuti Ine ndikuyenera kukhala pa ntchito ya Atate Anga?” Mawu akukona cholakwikacho. Mwaona, ndipo Chauzimu, Mwana wa zaka thwelovu zakubadwa! Ine sindikuganiza kuti Yesu ankamvetsa zimene Iye ankanenazo, koma Iye anali Mawu, ndipo Mawu amakonza cholakwika. Mwaona, Iye anawakonza amayi Ake, ndipo anawadzudzula iwo ponena zimenezo. Tsopano, ngati izo zikanakhala kuti—akanakhala pa ntchito ya abambo Ake, Iye akanakhala ndi abambo Ake, ngati Yosefe anali abambo Ake.

<sup>49</sup> Koma, mwaona, iye yense atang'ambika ndi kukondwa, monga Eva anali, ndi kukopedwa, chifukwa chiyani, iye anati, “Abambo Ako ndi ine takufunafuna Iwe, ndi misonzi.”

<sup>50</sup> Iye anati, “Kodi inu simukudziwa kuti Ine ndikuyenera kukhala pa ntchito ya Atate anga?” Mwaona momwe Mawu aliri okonza, Iwo amakonza cholakwikacho.

<sup>51</sup> Satana analakwitsa pamene anayesera kuti amuyese Yesu. Koma Iye anabwerera ndi Mawu Ake Omwe, ndipo anamugonjetsa iye ndi Mawu.

<sup>52</sup> “Mulungu,” Baibulo linanena apa, “mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyanasiyana, ankazidzindikiritsa Iyemwini kwa aneneri Ake, Iye

ankayankhula kwa makolo kudzera mwa aneneri.” Tsopano, powonetsera khalidwe Lake la kudzizindikiritsa Yekha, mwaona, kwa munthu, Iye ankayankhula kwa aneneri. Aneneri, masomphenya awo, akatsimikiziridwa, limakhala—limakhala khalidwe la Mulungu likudziwika ndi masomphenya a mneneriyo.

<sup>53</sup> Tsopano, palibe munthu angakhoze kufotokoza masomphenya, palibe njira yochitira izo. Ndi chazimu. Ndi chinachake chimene iwe umawona chomwe chakhala chiri, chimene chiri, ndi chimene chidzakhale. Ndipo iyo inali njira ya Mulungu, yomutumizira munthu amene ankayankhula zinthu zimenezo ndi kuwonetsera zinthu zimene zikanadzachitika (osati usikuuno wokha) usiku uliwonse, nthawi iliyonse. Chirichonse chimene iye ankanena chinkayenera kukhala mwangwiro ndi Ambuye, chinkayenera kukhala Mawu a Ambuye.

<sup>54</sup> Mwa ichi, mphatso ndi mayitanidwe ndi sizimasowa kulapa. Simungathe kuwapanga maso anu kukhala abulauni pamene iwo ali a buluu. Inu simungathe kudzipanga nokha a mapazi sikisi pamene muli a mapazi foro okha. “Ndani polingalira angawonjezere nkono umodzi ku usinkhu wake?” Ife tiri, tonse, chimene ife tiri mwa chisomo cha Mulungu.

<sup>55</sup> Tsopano, mphatso ndi mayitanidwe nzopanda kulapa. Aneneri awa ankabadwa aneneri. Mose anabadwa ali mwana wabwino. Yesu anali Mwana wa Mulungu, kuchokera pamene maziko a dziko lapansi anali asanakhazikitsidwe, chikhumbo cha Mulungu. Yeremiya . . . -thwelovu, zaka seveni handiredede ndi thwelovu, ine ndikukhulupirira izo zinali, iye asanabadwe, iye anali liwu la mmodzi, ayi, ndikupempha chikhululukiro chanu, iye anadzozedwa kukhala mneneri kwa mafuko, ndipo anali—ndipo anayeretsedwa m’imba mwa amayi ake ndipo anadzozedwa kuti adzakhale mneneri wa fuko. Yohane M’batizi, chimene ine ndikuganiza, pokhala zaka seveni handiredede ndi thwelovu iye asanabadwe. Iye anali liwu la iye wofuula m’chipululu.

<sup>56</sup> Mwaona, ndi Mulungu akukhazikitsa. Iye amamutumiza munthu, amakatenga Mawu a m’badwo umenewo. Koma tsopano inu musanakhulupirire Mawu amenewo a m’badwo umenewo, Iye amadzizindikiritsa Iyemwini mu khalidwe Lake, mwaona, mwa chidziwitso, mwa masomphenya. Iye ankanena zinthu zimene zikanadzachitika, ndipo izo zimadzachitika. Ndipo Mulungu anati, “Pamene izo zichitika, ndiye inu mukhulupirire kuti iye ali ndi kutanthauzira kwa Mawu, chifukwa Mawu a Ambuye akudza kwa munthu uyu.” Ndipo zomuyenereza zake: iye amazindikiritsidwa pokhala mpenyi, mu Chipangano Chakale. Zomveka basi momwe zingakhalire! Makhalidwe ake amazindikiritsa, kudziwitsidwa, makhalidwe ake.

<sup>57</sup> Tsopano, umo ndi momwe “Mulungu ankachitira mu nthawi zamakedzana,” Baibulo limati, “mmachitidwe osiyanasiyana, Iye ankayankhula ndi makolo kudzera mwa aneneri, koma mmasiku otsiriza ano kudzera mwa Yesu Khristu, Mwana Wake, Iye akuyankhula.”

<sup>58</sup> Tsopano, Yesu anati, mu Yohane 10:37, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine.”

Mwaona, iwo anati, “Iwe ndi Munthu, ndipo ukudzipanga Wekha kukhala Mulungu.”

<sup>59</sup> Iye anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine.” Tsopano Iye anati, “Yohane anali kuwala konyezimira ndi kowala. Inu, wamkulu, mumakonda kuyenda mu kuwala kwake kwa kanthawi. Tsopano Yohane anati, ‘Ine ndikuyenera ndichokepo; Iye akuyenera akule.’” Iye anali Kuwala kwa dziko lapansi, chifukwa Iye anali Mawu otsimikiziridwa, ozindikiritsidwa atasandulika thupi. Mwaona, Iye anali Mulungu nafe.

<sup>60</sup> Aneneri anali Mulungu ali ndi iwo. Yesu ananena chomwecho. Iye anati, “Ngati mumawatcha iwo amene Mawu a Mulungu amadza kwa iwo, ‘milungu,’ mukunditsutsa Ine bwanji pamene Ine ndikuti Ndine Mwana wa Mulungu?” Mukuona? Koteru pamene Mawu amene anayankhulidwa ndi Mulungu atsimikiziridwa, ndiye ameneyo ndi Mulungu akudzidziwitsa Iyemwini mwa khalidwe Lake, akukwaniritsa Mawu Ake. Iwo samasowa kutanthauzira. Iwo adzitanthauzira kale, Iwoeni, kutsimikizira chimene Iwo ali.

<sup>61</sup> Chimodzimodzi basi monga momwe Iye ananenera, “Kukhale kuwala,” ndipo panadzakhala kuwala, simungasowe kunena kuti, “Chabwino, kodi zimenezo zinatanthauza chiyani?” Izo basi zikutanthauza, ndi zimenezo pamenepo, izo zikutsimikizira izo. Izo zadzachitika kale.

<sup>62</sup> Tsopano Yesu ananena kuti, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga,” kapena mwakunena kwina, “ngati Ine ndiribe khalidwe la Atate Anga, musakhulupirire zimenezo. Izo zikuzindikiritsa khalidwe Langa, Yemwe Ine ndiri. Ngati inu simungandikhulupirire Ine, ndiye mukhulupirire chizindikiritso chimene Mulungu wapereka. Ngati inu—ngati inu simutero. . . Ngati Ine sindikutero, ngati khalidwe Langa silikuzindikiritsa malo Anga, ndiye musakhulupirire zodzinenera Zanga.” Mukuona? Inu mukumvetsa izo usikuuno? Ndi angati akumvetsa zimenezo, kwezani dzanja lanu. Mukuona? “Ngati khalidwe Langa silikuzindikiritsa Yemwe Ine ndimadzinenera kuti ndiri,” anatero Yesu, “ndiye inu mukhulupirire a. . . Ngati inu simungathe kundikhulupirira Ine, bwanji, mungokhulupirira a—a—chizindikiritso cha khalidwe limene Ine ndiri.”

<sup>63</sup> Yohane 14:12, “Iye amene akhulupirira” anatero Yesu “pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Tsopano penyani, “Iye amene akhulupirira pa Ine,” wokhulupirira woona, “ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Zindikirani. Mwa kuyankhula kwina, monga chonchi, “Iye amene akhulupirira pa Ine, adzazindikiritsidwa ndi khalidwe Langa, ntchitozo.” Tsopano, icho ndi chimene Iye anachita. Iye anati, “Ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate, ndiye musandikhulupirire Ine.” Ndipo Atatewo ankayankhula kwa aneneri, ndipo limenelo limakhala khalidwe lawo, chizindikiritso. Ndi mmenenso zimakhallira ndi Yesu. Ndipo analonjeza izo kwa iye amene akhulupirira, “Makhalidwe Anga azidzachita mwa iye monga momwe iwo ankachitira mwa Ine. Ndipo ngati Ine sindikuchita ntchito za Atate Anga, ndiye musandikhulupirire Ine. Koma ngati Ine ndikuchita ntchitozo, ndipo inu simungandikhulupirire Ine, ndiye mukhulupirire ntchitozo, chifukwa izo zinanenedwa, izo zikuyenera kukhalapo.”

<sup>64</sup> Iye anati, “Fufuzani Malemba, pakuti mwa Iwo inu mumaganiza kuti muli nawo Moyo Wamuyaya, ndipo Iwo ndi Iwo amene akukuuzani inu Yemwe Ine ndiri.” Ameneyo anali Yesu, mwaona, Mulungu akuwonetseredwa, akudziwonetsera Iyemwini. “Iwo akuchitira umboni Yemwe Ine ndiri.” Izo zikupanga Ahebri 1:1 tsopano, “Mulungu mu nthawi zamakedzana ankayankhula kudzera mwa aneneri,” kuzindikiritsa momveka tsopano khalidwe la chiwukitsiro cha Mwana Wake. Mulungu ankayankhula mwa aneneri nthawi imeneyo, kupyolera mwa Mwana Wake tsopano. Mulungu wosasintha, khalidwe lomwelo, “Ntchito zimene Ine ndikuchita, inunso mudzazichita.” Mulungu, wodziwika ndi khalidwe Lake lozindikiritsidwa. Umo ndi momwe inu mumadziwira.

<sup>65</sup> Inu mumati, “Chabwino, ine ndikukuuzani inu *izi*, ife timayimba *izi*, ife timachita *izi*, ndipo ife timachita.” Izo si zimene ine ndikunena.

<sup>66</sup> Ine ndikuyankhula za Mawu akuwonetseredwa ndi kuzindikiritsa a . . . ndi izo, makhalidwe a Mawu olonjezedwa a m’badwo.

<sup>67</sup> Afarisi amenewo ankalidziwa bwino Baibulo limenelo monga aliyense, mwabwino kuposa momwe aliyense wa ife akulu ampingo timalidziwira lathu lero. Iwo ankayenera kumakhala moyo mwa Ilo. Agogo a agogo awo anali ansembe. Iwo ankaliphunzira Ilo, usana ndi usiku, ndipo iwo analephera kuwona Mawu ozindikiritsidwa amenewo.

<sup>68</sup> Lero, Luther anati, “Pamene inu mukhulupirira, inu muli nawo Iwo.” Amethodisti amati, “Pamene inu mwafuula, inu muli nawo Iwo.” Achipentekoste anati, “Pamene inu munayankhula mmalirime, inu munali nawo Iwo.” Ife tikuzipeza zonsezo

kukhala zolakwika! Ena a iwo anati, “Chipatso cha Mzimu chiri nawo Iwo.” Ndipo izo nzolakwika! Umboni wokhawo ulipo, ndi pamene chitsimikiziro, pamene Mulungu Mwiniwake adzizindikiritsa Iyemwini mu Mawu olonjezedwa a oralo. Ndi zimenezotu.

<sup>69</sup> Ndi ndani amene anali ndi zipatso zambiri za Mzimu kuposa ansembe achifundo akale aja, ankawadula ana ndi kuwadalitsa iwo, ndi china chirichonse? Ndipo apa munthu uyu Yesu anali, anabwera pamenepo, anadzamenya theche pa midadada yawo ya nsembe, anayang’ana pa iwo ndi mkwiyo, kuwamenya iwo, kuwathamangitsira iwo panja, opanda chizindikiritso cha chirichonse. Lemba ndicho chizindikiritso Chake! Iye analibe khadi la chiyanjano, Iye sanali wa bungwe lirilonse. Koma Mulungu anayankhula za Iye, icho chinali chizindikiritso Chake!

<sup>70</sup> Icho chimakhala chizindikiritso chenicheni cha Mulungu mu ora lirilonse, ndicho chizindikiritso Chake. Ndicho chimene icho chiri, Malemba amene analonjezedwa, atazindikiritsidwa ndi chikhalidwe cha lonjezo limene liri Mulungu, ndipo Mulungu ndi Mawu. Ndipo khalidwe la lonjezo limenelo likuzindikiritsidwa, izo zimamupanga wokhulupirira. Yesu ananena chomwecho, ndipo izo zikukhazikitsa izo. Amen.

<sup>71</sup> Zindikirani, tsopano ife tikupeza, zikhalidwe zimamuzindikiritsa Iye. “Ngati...” Iye anati, “Ngati izo sizichita izo, ndiye musandikhulupirire Ine.” Tsopano, Yesu anayankhula kuti izo zikanadzamuzindikiritsa Iye.

<sup>72</sup> Ndipo tsopano kumbukirani, kuti mmasiku awa, masiku otsiriza ano, anatero Ahebri 1:1, “Mulungu, mu nthawi zamakedzana ndi mmachitidwe osiyanasiyana, ankayankhula kwa makolo kudzera mwa aneneri. Mu tsiku lotsiriza lino wayankhula kwa ife kupyolera mwa Mwana wake, Yesu Khristu.” Mukuona? Kuzindikiritsidwa kwa Mulungu Mwiniwake kukuwonetseredwa mu kachitidwe komweko monga momwe Iye anachitira mmbuyomo, pogwiritsa ntchito khalidwe Lake lomwelo. Amen. Zindikirani Ahebri 13:8, amati, “Iye ali yemweyo dzulo (nthawi zamakedzana), lero, ndi kwanthawizonse yemweyo!” Machitidwe Ake omwewo, njira Yake yomweyo, khalidwe Lake lomwelo, chirichonse ndi chofanana! Mulungu, Mulungu wasasinthika sangathokere kuchoka ku khalidwe limenelo monga momwe Iye sangachokere ku lamulo Lake. Ndicho chimene Iye ali, Iye ndi Mawu. Iye ndi Mawu a orali. Iye ndi Mawu. Pamene Iye analenga dziko, amenewo anali Mawu. Pamene Iye anamulenga munthu, ameneyo anali Mawu, zikhumbo Zake. Pamene Iye anamulenga Khristu, ameneyo anali Mulungu, Emanuele. Ndipo pamene Iye anamupanga Iye Mpulumutsi, izo zinali zikhumbo Zake. Pamene Iye anamupanga Iye Mchiritsi, izo zinali zikhumbo Zake. Mukuona? Ndi Mawu nthawizonse akuzindikiritsidwa, Mawu

ozindikiritsidwa ndi chikhalidwe cha Mulungu. Zindikirani machitidwewo, Iye nthawizonse, Iye samasintha nkomwe.

<sup>73</sup> Tayang'anani pa amuna atatu amene anabwera kwa Abrahamu, atakhala pakhomo la chihema chake tsiku limenelo. Tiyang'ana pa iye pamenepo kwa maminiti angapo. Iye anali atabwera, iye anali atayitanidwa kutuluka m'dziko la Akasidi, Akasidi, ndi mzinda wa Uri. Iye anali atapititsidwa kunja kwa mzinda wake, mwa malamulo a Mulungu, kuti iye adzipatule yekha ku kusakhulupirira konse. Limenelo ndiro khalidwe loyamba la Mulungu, kudzipatula wekha ku kusakhulupirira, pamene Iye amuyitana munthu!

<sup>74</sup> Ndipo Iye anamupatsa iye chinachake chimene chinali mwamtheradi, chosatheka kwathunthu kwa malingaliro achibadwa, kuti achikhulupirire icho. Iye anati, "Abrahamu, wako..." Anali ndi zaka sevente-faivi, ndipo Sarah anali ndi zaka sikisite-faivi. Iwo, ameneyo anali mlongo wake watheka, iwo anali atakhala pamodzi zaka zonsezo opanda mwana. Iye anati, "Ndidzakupatsa mwana wamwamuna mwa Sarah, ndipo iye adza, mwa iye, Ine ndidzakupanga iwe atate wa mafuko ambiri." Tsopano, iye anakhulupirira izo.

<sup>75</sup> Nthawi inadutsa, panalibe kusintha mwa Sarah. Mukuona? Iye anali atadutsa usinkhuwo, iye—iye anali atadutsa usinkhu wa kusintha kwa thupi. Sikisite-faivi, iye anali atadutsa kale nthawi imeneyo. Abrahamu, sevente-faivi, thupi lake chimodzimodzi ngati lakufa. Mimba yamkaziyo inali chimodzimodzi ngati yakufa. Koma Abrahamu sanadzandime konse pa lonjezo la Mulungu, kupyolera mu kusakhulupirira. Iye anapitiriza kukhulupirira, chifukwa Mulungu ananena zimenezo, ndipo anakopeka, "Ngati Mulungu ananena izo, makhalidwe Ake adzatulutsa chimene Iye ananena!" Tsopano, ife tikuyenera kukhala ana a Abrahamu, Mbewu ya Abrahamu! Anapitirira, anapitirira, zaka twente-faivi zinadutsa. Panalibe kusintha mwa Sarah, panalibe, kokha kuti iye anali wokalamba kwambiri, anawerama pansi, ndipo iye nayenso. Komabe Abrahamu anakhulupirira zimenezo.

<sup>76</sup> Ndipo tsiku lina, pamene Mulungu anawona kuti wantchito Wake anali atatsimikiza kuti akhala chitsanzo kwa anthu a lero, ndipo kudzera mwa iye Iye anali woti adzadalitsa mafuko, mmawa wina wotentha pafupifupi leveni koloko, amuna atatu anabwera akuyenda kudzafika kwa iye. Iwo anayankhula naye iye. Ndipo anawayitanira iwo mkati kuti akhale pansi. Panali chinachake chokhudza iwo chimene chinkawoneka chosiyana ndi munthu. Zinthu zauzimu zimamvetsetseka ndi zinthu zauzimu. Zindikirani, ndipo iwo anabwera ndipo anadzakhala pansi. Abrahamu anawayang'ana iwo, iye anati, "Ambuye wanga." Kodi iye akuyenera achite chiyani?

<sup>77</sup> Awiri a iwo anatsikira kumusi ndipo anakalalikira mu

Sodomu, umene uli umboni wamakono lero. Ndi amenewo magulu anu atatu a anthu: Sodomu, ndi mpingo uko mu Sodomu, Abrahamu Wosankhidwayo siali mu Sodomu. Amithenga awiri, Billy Graham wamakono ndi . . . Kumbukirani, mwa atumiki onse ku mpingo, sipanayambe pakhalapo munthu amene anayamba watulukapo mu mpingo umenewo mwadzina kunja uko, womalizira dzina lake ndi h-a-m, kale. Kwakhala kuli Finney, Sankey, Knox, Calvin, ndi ena otero, Billy Sunday, ndi china chirichonse, koma osati G-r-a-h-a-m, kapena aliyense wothera ndi h-a-m, zomwe zimatanthauza “atate wa mafuko.” Kumeneko iye anapita kumeneko, akulalikira. Tayang’anani pa oralo! Apa pali odzipangitsa-kukhulupirira, osakhulupirira, ndi okhulupirira. Amuna atatu awa anabwera. Awiri a iwo anapita uko mu mzinda, Billy Graham wamakono ndi Oral Roberts kumusi pakati pa anthu, akulalikira. Mmene zinakhallira, Yesu analozera kwa zimenezo.

<sup>78</sup> Zindikirani, Osankhidwa anabwera pa . . . atakhala kunja kumtunda kuno, Abrahamu ndi gulu lake. Ndipo pamene Munthu uyu amene anakhala ndi Abrahamu, muwonezi Iye, Iye anawonetsera khalidwe la Mulungu, pakuti Iye anati, “Sarah ali kuti?” Dzina lake linali Sarai, dzulo lake; tsopano ndi Sarah, S-a-r-a-h. Anati “Abrahamu,” osati Abram, “Abrahamu, ali kuti mkazi wako, Sarah?”

Anati, “Iye ali mu hema kumbuyo Kwanu.”

<sup>79</sup> Anati, “Ndidzakuchezerani inu.” Kenako Abrahamu anamvetsera ku kuyankhula kumeneko. “Ndidzakuchezerani inu molingana ndi nthawi ya moyo.”

<sup>80</sup> Ndipo Sarah anaseka, monga mmene zinakhallira, mwachinunu, kwa iyemwini, ndipo anati, “Ine wokalamba, ndipo mbuye wanga wokalamba, kuti tidzasangalalenso ngati anyamata ndi atsikana? Monga momwe a—monga ubale waumunthu, mwinamwake, zadutsa zaka zambiri. Ine?” Iye anaseka.

<sup>81</sup> Ndipo Munthuyo, akuyang’ana pa Abrahamu, Sarah ali mu hema kumbuyo kwa Iye, anati, “Nchifukwa chiyani Sarah anaseka, ponena izi, ‘Kodi zinthu zimenezi zingatheke bwanji?’” Iye anadzizindikiritsa Iyemwini.

<sup>82</sup> Ndipo Abrahamu anamutcha Iye “Elohim.” Tsopano, aliyense wa inu owerenga Baibulo mukudziwa zimenezo. Elohim, Mulungu, Mmodzi Wokwanira mu Zonseyo, mwaona, atazindikiritsidwa mu thupi la munthu amene anali kudya nyama ya ng’ombe, akumwa mkaka wa ng’ombe, ndi kudya mkate ndi batala. Elohim anazindikiritsa makhalidwe a Mulungu, ndipo Abrahamu anamutcha Iye “Mulungu.” Chiyani? Iye anazindikiritsidwa, Elohim!

<sup>83</sup> Yesu ananena, mu Luka, mutu wa 17, pamene mmasiku otsiriza (Mulungu mu nthawi zamakedzana akuyankhula

mwa aneneri, mmasiku otsiriza mwa Mwana Wake), tsopano penyani, Iye anati, “Mu nthawi imene Mwana wa munthu adzawululidwa.” Penyani, “kuwululidwa,” kuzindikiridwa mmasiku otsiriza ano isanafike nthawi yotsiriza, pamene Mwana wa munthu adzawululidwa, mmene zinakhalira ku Sodomu zidzabwereranso kachiwiri. “Monga zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhalanso pa kudza kwa Mwana wa munthu, pamene Iye azidzawululidwa, kudziwitsidwa kwa Mpingo, kwa Osankhidwawo (osati ku Sodomu kapena Achisodomu, kapena awo uko mu Sodomu), kwa Osankhidwa.” Abrahamu anali Wosankhidwa. Ndipo Mbewu yachifumu ya Abrahamu ndi okhulupirira, kudzera mwa Khristu Yesu Mawu, ndipo ndi Osankhidwa. Ndipo pamene Mwana wa munthu akuwululidwa, mmene zinakhaliramo zidzakhalanso kachiwiri.

<sup>84</sup> Tayang’anani pa dziko lapansi lero. Ngati si Sodomu ndi Gomora wawamba, ine sindinayambe ndamuwonapo mmodzi. Sodomu ndi Gomora! Tayang’anani pa mpingo, monga Loti atakhala pamenepo ndipo kumangowumvetsa chisoni moyo wake wolungama pamene iye ankawona machimo a Sodomu. Atumiki ambiri atakhala mwa mwake... Bambo wabwino atakhala mowerengera mwake, akutenga phunziro lake ndi zina zotero, akuyang’ana kunja pa msewu ndi kumawona akazi atavala akabudula, ndi zopanda makhalidwe ndi zinthu, ndi zinthu zikuchitika monga chomwecho, iye sakananena kanthu za zimenezo, bungwe lake likanakhoza kumutulutsa iye panja. Loti analibe kulimba mtima kuti ayimirire Chimene chinali cholondola, momwemonso ndi Sodomu ndi Gomora wamakono lero.

<sup>85</sup> Koma pali ena a iwo amene ali kunja kwa Sodomu, amene anabadwira kunja uko, osati mwa chifuniro cha munthu, koma mwa chifuniro cha Mulungu ndi Mbewu ya Mulungu. Penyani chizindikiritsocho pamenepo, osati kungolalikira chabe, koma chizindikirocho chinazindikiritsa Mawu a Mulungu atapangidwa thupi mwa munthu. Mmene zinakhaliramo zikubwereranso monga izo zinachitikira, ndipo ndizo ndendende tsiku limenelo. Chirichonse ndi changwiro, chirichonse chiri mu mzere kumene. Ndikanakonda tikanakhala ndi nthawi kuti tizipitiriza pa izo maminiti pang’ono, koma ife tiribe, kotero ife tifulumira. Mmene zinakhaliramo ndi zakuti zidzabwezeretsedwanso mmasiku otsiriza.

<sup>86</sup> Tsopano, Ahebri 10:1, “Mulungu, mu nthawi zamakedzana, mwa aneneri, ankadzizindikiritsa Iyemwini. Ndipo mmasiku otsiriza kudzizindikiritsa Iyemwini kupyolera mwa Mwana,” kumupanga Iye Ahebri 13:8, “yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

<sup>87</sup> Zindikirani, Mulungu, mu nthawi zamakedzana, ankayankhula kwa Mose. Ndipo tsopano, ndipo kumbukirani, Iye anazidzindikiritsa Iyemwini ndi Kuwala, Lawi la Moto mu

chitsamba chonyeka. Umo ndi momwe Iye ankachitira izo mu nthawi zamakedzana. Ndipo Iye anayankhula ndi Mose. Ndipo Kuwala kumeneko, kodi Iko kunachita chiyani? Iko kunabala khalidwe la Mulungu, Iko kunayankhula Mawu, “Ine ndamva kubuula kwa anthu Anga mu Igupto. Ine ndawona kubuula kwawo ndipo ndamva kulira kwawo, ndipo Ine ndakumbukira Mawu Anga. Ine nditsikira kumeneko, Lawi la Moto, Kuwala, kuti ndipite ndi kukawombola anthuwo. Ine ndikukutuma iwe, Mose.”

<sup>88</sup> Penyani makhalidwe a Mulungu. Anatenga fumbi lodzaza dzanja ndi kuliponya mu mlengalenga, ndipo ilo linasanduka utitiri. Khalidwe la Mlengi wa Mulungu linali mwa Mose.

<sup>89</sup> Ndipo Mose anayankhula, mu Deuteronome 18:15, ndipo anati, “Ambuye Mulungu wanu adzadzutsa Mneneri wonga ine.” Tsopano penyani, amenewo ndi Mawu kachiwiri, khalidwe. Mulungu akuyankhula kudzera mwa Mose, akuwauza iwo kuti Ambuye akanadzadzutsa Mmodzi wonga iye. Tsopano zindikirani momwe makhalidwe a Yesu anamuzindikiritsira Iye kukhala Mawu olonjezedwa awa. Pamene Mose ananena kuti izo zikanadzakhala, khalidwe la Yesu linazindikiritsa izo. Zindikirani tsopano, “Ambuye Mulungu wanu,” ameneyo ndi Mulungu, amenewo ndi Mawu, “adzautsa Mneneri wonga ine. Aliyense amene sadzakhulupirira Mneneri ameneyo, adzadulidwa pakati pa anthu.” Tsopano penyani, pamene Yesu anabwera, ndiye ndi khalidwe la mtundu wanji limene Iye ankayenera kuti akhale nalo? Mwaona, zindikirani tsopano Mawu olonjezedwa, Iye analonjezedwa kudzakhala Mneneri wonga Mose.

<sup>90</sup> Tsopano, iwo anakhala ndi aphunzitsi amitundu yonse, marabi amitundu yonse. Iwo anali asanakhale ndi mneneri kwa zaka foro handirede, kuyambira—kuyambira pa Malaki, ndipo tsopano zonse mwakamodzi apo panadzabwera Munthu powonekera.

<sup>91</sup> Tsopano, panali nsodzi, awiri a iwo, ana aamuna a munthu, ndipo mmodzi wa iwo, dzina lake linali Andrea, ndipo dzina la winayo linali Simoni. Iwo anali atawuzidwa ndi abambo awo momwe akanati aziyang’anira mmasikuwo; panali zinthu zambiri zabodza zomwe zinawukapo. Munthu wachikulireyo. . . Ine ndinawerengapo bukhu laling’ono nthawi ina, kumene, mwina zinali zopeka, ine sindikudziwa, kuti iye anati, “Ana, tsopano Mesiya asanabwere, monga ife tonse tikumuyembekezera, padzakhala nthawi imene padzakhale mitundu yonse ya zinthu zikuchitika. Koma momwe inu muti mudzamudziwire Mesiya uyu, Iye adzakhala molingana ndi Lemba. Iye adzakhala Mneneri, chifukwa Mawu a Mulungu anati Iye ndi Mneneri.”

<sup>92</sup> Andrea anamumva Yohane. Chabwino, chinthu chokhacho

chimene Yohane ankachita, chinali kungonenera. Inu mukudziwa, Yesu anati, “Inu munayenda mu kuwala kwa Yohane, koma Ine ndiri ndi kuwala kwakukulu kumuposa Yohane. Ine ndiri ndi chizindikiritso chachikulu kuposa Yohane, pakuti, ntchito zimene Atate anandipatsa Ine kuti ndidzachite, izo zikuchitira umboni za Ine.” Yohane anangolalikira, iye anangotsogolera, iye sanachite zozizwitsa zirizonse kapena makhalidwe aliwonse a Mulungu kwa lonjezolo. Koma apa panadzabwera Yesu ali ndi khalidwe limenelo!

<sup>93</sup> Simoni anapita kumeneko kuti akamumvetsera Iye tsiku lina, ndipo mwamsanga pamene... Simoni mwinamwake anapita ndi Andrey. Andrey anali akupezekako nthawi yonseyo. Koma, Simoni, pamene iye anabwera mu Kukhalapo Kwake! Tsopano mvetserani, pamene tikutseka. Pamene iye anabwera mu Kukhalapo kwa Yesu, Yesu anayang’ana pa iye, Iye anati, “Dzina lako ndi Simoni, ndipo ndiwe mwana wa Yonasi.” Mwaona, khalidwe la zomwe zinalonjezedwa linazindikiritidwa mwa Iye.

<sup>94</sup> Munthu ameneyo samakhoza kulemba dzina lake, Baibulo linati iye anali zonse mbuli ndi wosaphunzira. Koma icho chinali chizindikiritso choterocho, mpaka kuti iye mwamsanga anakana kusakhulupirira kwake konse, ndipo iye anati, “Ameneyo ndi Mesiya amene ife takhala tikumuyembekezera!” Chabwino, iye anazikhulupirira Izo.

<sup>95</sup> Panali wina atayima pamenepo, dzina lake Filipino, amene anathamanga kuzungulira mzindawo, phiriro, dzikolo, pafupifupi mamailosi fifitini, ndipo anakamupeza mzake, anabwereranso tsiku lotsatira ndi iye, dzina lake Nataniele. Iye anamupeza iye ali panso pa mtengo, akupemphera. Iye anati, “Bwera, udzawone Amene ife tamupeza, Yesu waku Nazarete, mwana wa Yosefe.”

<sup>96</sup> Iye anati, “Tsopano, tsopano, tsopano! Kodi pangakhale chinthu chabwino chirichonse chochokera ku Nazarete, kuchokera mu gulu limenelo la anthu otsika kumusi uko?”

Iye anati, “Bwera ndipo udzawone!”

<sup>97</sup> Ndicho chopambana—ndiyo ndemanga yabwino kwambiri imene munthu anganene. Osakhala kunyumba ndi kumatsutsa. Bwerani ndipo mudzafufuze, fufuzani Malemba! Bwerani, mudzawone!

<sup>98</sup> Panjira yozungulira, iwo anali akuyenda, akuyankhula za zimene zinakhala zikuchitika, momwe iye anamuwuzira iye za Simoni atadziwidwa ndi Iye, abambo ake ndi zina zotero.

<sup>99</sup> Kenako pamene iye anafika mu mzere, mwinamwake unali mzere wa pemphero, akhoza kukhala kuti anali kunja mwa omvetsera, ine sindikudziwa. Koma kulikonse kumene iye ankachokerako, ndipo Yesu anaika maso ake pa iye

nthawi yoyamba, Iye anati, “Taonani M’israeli, amene mwa iye mulibemo chinyengo!”

Iye anati, “Rabbi, Inu munandidziwa ine liti?”

<sup>100</sup> Iye anati, “Filipo asanakuyitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.” Chimenecho chinali chizindikiritso cha makhalidwe a Mulungu wodzozedwa.

<sup>101</sup> Anati, “Rabbi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu!” Icho chinali chiyani? Makhalidwe Ake anamuzindikiritsa Iye. Iye anadziwa mwa Lemba kuti uyo anali Munthu wodzozedwayo, Mulungu wodzozedwa mthupi. Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjani dziko lapansi kwa Iyemwini. Iye anati, “Rabbi, Inu ndi Mwana wa Mulungu. Inu ndinu Mfumumu ya Israeli.”

<sup>102</sup> Yesu anati, “Chifukwa Ine ndanena zimenezo, iwe ukundikhulupirira Ine? Iwe udzawona zazikulu kuposa izi.”

<sup>103</sup> Tsopano, panali iwo amene anayima chapafupi, sanakhulupirire Izo. Iwo anati, “Munthu uyu ndi Bezebule, Iye ndi wam’bwebwe.”

<sup>104</sup> Yesu anati, “Ine ndakukhulukirani inu chifukwa cha zimenezo. Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera kudzachita chinthu chomwecho, mawu amodzi otsutsa Iwo sadzakhulukidwa konse mu dziko lino kapena mdziko lirinkudza.”

<sup>105</sup> Mwaona, chitetezero chinali chisanapangidwebe. Mwaona, sipakanakhoza kukhala, inu simungakhale... Inu simungaponyedwe mu gehena musanabwere mu chiweruzo. Fuko ili silingachite zimenezo, Mulungu sangatero nayenso. Mwaona, inu muli pamalo, mukuyembekezera mmaunyolo a ndende mpaka mudzalandire chiweruzo. Ndipo, inu mwaona, Iye sakanakhoza kuwathamangitsa iwo, chifukwa chitetezero chinali chisanapangidwebe.

<sup>106</sup> Koma itachitika imfa Yake, kuyikidwa mmanda, ndipo Chizindikiro chinabwerapo kuchokera m’Magazi, Mzimu Woyera, ndiyeno, kuyankhula motsutsa Iwo, ndi tchimo losakhulukidwa. Mawu amodzi okha basi ndi omwe inu mukuyenera kunena motsutsa Iwo, ndiye sipangakhaleenso chikhulukiro paliponse. Mawu amodzi otsutsa Iwo, mwaona, ndi chinthu chachikulu bwanji chimene icho chiri.

<sup>107</sup> Tsopano, kotero ndiye ife tikupeza kachiwiri, ichi chinamuzindikiritsa Iye monga Mesiya wodzozedwa. Mulungu mwa Khristu, Chitetezero cha masiku otsiriza, Khristu akupanga chitetezero cha masiku otsiriza. Tsopano, kwa Nataniele, iye—iye—iye anawakhulupirira Iwo ndipo anamuzindikira Iye.

<sup>108</sup> Panali mkazi wamng’ono amene anabwera ku chitsime nthawi ina uko ku Sukari, mzinda wa—waku Samariya. Yesu ankayenera kuti apite kumeneko pamene Iye anali pa njira

Yake akupita kumusi, kumusi komwe kwa phiri kuchokera ku Yerusalemu, mpaka ku Yeriko, koma Iye anazungulira ku Samariya. Anati Iye anali “kusowekera kuti apite,” Atate anamutsogolera Iye kumeneko. Pamene Iye anapita kumeneko, Iye anawatumiza ophunzira kutali. Ndipo anakhala pansi, akudabwa, ine ndikuganiza, chimene icho chinali.

<sup>109</sup> Tsopano kumbukirani, Yohane Woyera 5:19, Yesu anati, “Indetu Ndinena kwa inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awona Atate akuchichita.” Tsopano kumbukirani, Iye sanachite konse chozizwitsa chimodzi, osati pamene Iye *anamva* icho, pamene Iye “anawona” icho. “Mwana samachita kalikonse mpaka Iye atawona Atate akuchichita icho poyamba.”

<sup>110</sup> Mwaona, izo zinawonetsera chimene Iye anali, Mneneri ameneyo, Mulungu-Mneneri. Woposa Mneneri, Iye anali Mulungu! Zonse zimene aneneri anali, zinali mwa Iye, kuwonjezerapo. Aneneri amangokhala ndi gawo chabe la Mawu. Iye anali ndi Mawu onse, Iye anali Mawu mu chidzalo Chake. Koma zindikirani, “Mulungu mu nthawi zamakedzana ankayankhula mu njira zosiyanasiyana, kupyolera m’timagawo ting’onoting’ono. Mu tsiku lotsiriza lino, chidzalo cha Mawu chabwera mwa Mwana Wake Khristu Yesu, Mulungu wosandulika thupi pakati pathu.”

<sup>111</sup> Mkazi wamng’ono uyu, wa mbiri yoyipa, ife timamutcha iye, nthawizina, hule. Mwinamwake mwanayo anali atasiyidwa mu msewu. Nthawizina monga pano, izo si ana olekerera kwenikweni, ndi makolo olekerera, kumulola dona wamng’onooyo kuti atuluke ndi kumachita monga chomwecho. Mwinamwake mkazi wamng’ono wokongola, iye anapita kumeneko kuti akatunge madzi mu chidebe, pafupifupi leveni koloko.

<sup>112</sup> Tsopano kumbukirani, ngati inu munayamba mwakhalapo kummawa, iwo sanasinthe ngakhale pang’ono, ikadali miyambo yomweyo. Akazi amatuluka, anamwali amalawirira ku chitsime ndi kukatunga madzi awo. Hule kapena wa mbiri woyipa sangapite ndi iwo. Iwo sangasakanizikane pamodzi.

<sup>113</sup> Iye ankayenera kuti atuluke ena onsewo akamaliza. Iye amabwera, mwinamwake atatopa, mwinamwake iye anali ndi bwenzi latsopano lija, mwamuna wake usiku umenewo. Iye anatulukira, anali ndi mtsuko wa madzi uwu, iye anawukhazika iwo pansi. Anayika icho, chotungiracho pansi, kuti achilowetse icho pansi, iye anamumva Mwamuna akuti, “Ndibweretsere Ine akumwa.”

<sup>114</sup> Iye anayang’ana apo ndipo iye anawona Mwamuna wa usinkhu wapakati atayima pamenepo, wokhala ngati wa imvi mu ndevu Zake. Iye anali pafupifupi usinkhu wa zaka sarte zokha, koma Baibulo linati Iye ankawoneka ngati wa fifite. “Iwe

ndi munthu wosapitirira usinkhu wa zaka fifite, ndipo ukuti Iwe unamuwona Abrahamu?”

115 Iye anati, “Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE.” Mukuona? Mwaona, iwo sanazimvetse Izo. Iye ankagwedeza tizirombo timenecho kuti tichoke kwa Iye.

116 Lero ife timayenera kuwapempha ndi kuwachonderera, ndi kuwasisita ndi kuwapempha, ndi kuwakopa ndi kuwalonjeza Akhristu, kuti abwere ku tchalitchi, “Ngati iwo abwera ku tchalitchi, ife tichita chakuti-ndi-chakuti.”

117 Yesu, pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anali ndi ochuluka ali ndi Iye. Iye anayang’ana pozungulira ndipo anawona osonkhana, Iye ankafuna kuti awachotse iwo, Iye anati, “Pokhapokha ngati inu mutadya thupi la Mwana wa munthu ndi kumwa Magazi Ake, inu mulibe Moyo mwa inu.”

118 Kodi mungalingalire dokotala atakhala kunjja uko? “Bwanji,” anati, “Munthu uyu akufuna kuti ife tikhale akudya anthu. Kumwa Magazi Ake? Zamkhutu! Anthu nonsenu chokaniko ndipo mumusiye Munthu wamisalayo yekha.” Iwo anachokapo.

119 Iye sanafotokoze konse Zimenezo. Iye sankasowa kuti afotokoze Zimenezo. Iye amagwedeza chikhulupiriro chanu nthawizina kuti awone chimene inu muti muchite. Ndipo Iye akuchita chinthu chomwecho mu tsiku lino, inde, kulola izo ziwoneke ngati zachilendo kwa inu pang’ono pokha, kuti awone pamene inu mwayima, ngati inu mumakhulupiradi kwenikweni.

120 Kumbukirani, iwo...-phunzira, odzozedweratu ndi Mulungu, sanasunthike. Iwo sakanakhoza kufotokoza Izo, ngakhalebe, koma iwo sanafune kuti asunthe. Ndiye Iye anabweranso kachiwiri, Iye anati. . .

Osonkhana onsewo anachokapo, masauzande.

121 Iye ananena kwa sevente atakhala pamenepo, atumiki Ake amene Iye anawadzoza kuti apite kunjja ndi kukalalikira pamaso pa Iye, Iye anati, “Ine ndiwagwedeza iwo ndi kuwona pamene iwo ali.” Koteri Iye anati, “Chabwino, inu mudzanena chiyani pamene mudzawona Mwana wa munthu akukwera Kumwamba kumene Iye anachokera?”

122 “Mwana wa munthu akukwera Kumwamba? Ife timawedza ndi Iye, timakhala m’mphepete mwa mtsinje limodzi ndi Iye. Ife timadya limodzi ndi Iye. Ife tinawona modyera ng’ombe mmene Iye anabadwiramo. Ife timawadziwa amayi Ake, achimwene Ake. Ndiye Mwana wa munthu uyu kukwera kumwamba kumene Iye anachokerako? Iye anachokera ku Nazareti! Awa ndi mawu olimba.” Iwo anachokapo, nawonso. Iwo anati, “Ife sitingamvetse Izi.” Inu mukuwona? Chinachitika ndi chiyani? (Sizinawasunthe konse ophunzira amenewo. Iwo sakanakhoza

kufotokoza Izo.) Onse a iwo anachokapo. Iye sanazifotokoze Izo. Iye sankasowa kutero.

<sup>123</sup> Lero ife tiri ndi mbewu zochita kupembedzedwa, zotchedwa Akhristu, winawake amene inu mumayenera kumupopera ndi kumunyengerera ndi kumuseketsa, “Ndipo kodi inu mundipatsa ine chiyanjano, kodi inu mugwirizana nawo, kodi inu muchita *ichi*?” Oh, inu mulu wa mbewu zochita kupembedzedwa! Ife tikusowa Chikhristu china chenicheni, chobadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Ndipo icho sichidzatenga mgwirizano, palibe china chirichonse, iwo samafuna chirichonse.

<sup>124</sup> Yesu anatembenuka, anayang’ana kwa ophunzira amenewo, anati, “Kodi inu mupita, nanunso? Kodi inu mukufuna kupita, nanunso?” Iye anati, “Ine ndasankha thwelovu a inu, ndipo mmodzi wa inu ndi mdierekezi. Bwanji inu osapita, nanunso?”

<sup>125</sup> Kenako Petro ananena mawu achikumbutso aja, “Ambuye, ife tingapitenso kuti? Ife takopeka, ife tikudziwa kuti Inu ndi Kasupe wozindikiritsidwa wa Moyo. Inu muli nawo Mawu, ndipo Iwo okha. Ife takopeka.”

Mkazi wamng’ono uyu atayima pamenepo. Anati, “Ndibweretsere ine akumwa.”

<sup>126</sup> Iye anati, “Si chamwambo, ife tiri ndi tsankho, ife tiribe chinthu choterocho kuno.”

<sup>127</sup> Iye anamulola iye kuti adziwe mwamsanga kuti palibe kusiyana pakati pa Myuda kapena chirichonse chimene chinali. Iye anali Mulungu. Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno.”

Iye anati, “Ine ndiribe mwamuna.”

<sup>128</sup> Iye anati, “Iwe wanena zooni. Iwe wakhala nawo faivi, ndipo amene iwe ukukhala naye tsopano si wako.”

<sup>129</sup> Tsopano muwoneni mkazi ameneyo. Chinachake chinachitika, Mbewu yaing’ono yokonzedweratu ija pansu mu mtima mwake!

<sup>130</sup> Pamene Iye ananena Izo kwa Afarisi aja, tayang’anani pa iwo, iwo anangodetsa chimene iwo ankadzinenera. Iwo ankadzinenera kuti ndi Akhristu, ankanena kuti ndi otsatira ake, ankanena kuti ankamukonda Iye. Koma pamene Choonadi chinabwera, Icho chinawadetsa iwo.

<sup>131</sup> Koma pamene *Ichi* chinabwera, Icho chinabweretsa ku Moyo, Icho chinachotsa mdima ndi kuwupanga iwo wonse kukhala woyera. Anati, “Kuti . . .”

<sup>132</sup> Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Tsopano, ife sitinakhale naye mmodzi kwa zaka foro handireded.” Mukuona? “Ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Tsopano, ife tikudziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, Chomuzindikiritsa

Chake chidzakhala mtundu umenewo wa chikhalidwe, Iye adzatiuza ife zinthu izi.”

Iye anati, “Ine ndi Iye amene ndikuyankhula ndi iwe.”

<sup>133</sup> Ndipo, pa zimenezo, iye anagwetsa mtsuko wa madziwo, analowa mu mzinda ndipo anati, “Bwerani, mudzawone Munthu amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi ichi si chikhalidwe kumene cha Mesiya wodzozedwa amene ali Mawu, amene amadziwa malingaliro amene ali mu mtima? Kodi uyu si Mesiya?” Oh, mai!

<sup>134</sup> Penyani, mkazi wa vuto la magari, Iye anazindikiritsidwa kwa iye, ndi khalidwe Lake, kuti Iye anali Mesiya. Mkazi wa vuto la magari anamuzindikira Iye, Mawu.

<sup>135</sup> Ahebri 4:12, Baibulo linanena kuti, “Mawu a Mulungu ndi amphamvu kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndi Ozindikira malingaliro amene ali mu mtima,” (Ndi angati akudziwa zimenezo?) “m’malingaliro.” Icho ndi chimene Mawu ali. Inu mukukhulupirira kuti Iye anali Mawu? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Uh-huh. Izo zikukhazikitsa izo, ngati inu mukukhulupirira Izo.

<sup>136</sup> Zindikirani, mkazi wamng’ono uyu anati, “Ngati ine ndingathe kungomukhudza Iye! Ine sindikusamala ndi zochuluka bwanji zomwe iwo amanena za Iye. Ine ndikukhulupirira kuti Iye ali basi chimene Iye ananena kuti Iye anali. Ngati ine ndingathe kumukhudza Iye, ine ndichiritsidwa.” Kotero iye anazembera ndipo anakamukhudza Iye. Anabwerera mwa omvetsera.

Yesu anayima, ndipo anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

<sup>137</sup> Ndipo Petro anayesera kumupanga Iye ngati kuti Iye anali wamisala, iye anati, “Bwanji, aliyense! Musanene zinthu ngati zimenezo, bwanji, iwo sadziwa choti aganize za Inu. Munthu wa ulemu Wanu, ndipo kenako nkunena kuti, ‘Ndani wandikhudza Ine?’ Aliyense akukukhudzani Inu.”

<sup>138</sup> Iye anati, “Koma Ine ndazindikira kuti ndafooka, ukoma wandichokera Ine.” Anadziwa kuti chinachake chinali chitachitika!

<sup>139</sup> Tsopano taonani, taonani chimene chikubwera, kugwedeza kwakukulu kotsatira. Iye anayang’ana pozungulira mpaka Iye anamupeza iye, ndipo Iye anamuza iye vuto lake, chikhulupiriro chake chinali chitamupulumutsa iye. Iye anali...Iye anazindikiritsidwa ngati Mawu a Mulungu, akudziwa zinsinsi zamu mtima. Oh, mai! Mawu amazindikira thupi, amazindikira mtima.

<sup>140</sup> Tsopano mphindi chabe, potseka. Tsopano, monga momwe Ahebri 13:8 aliri wona, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse,” kodi inu mukukhulupirira Zimenezo?

Tsopano ine ndikusiya zambiri apa zomwe ndimayenera kuzinena. Ndiye, khalidwe Lake limuzindikiritsa Iye tsopano mu nthawi ino, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, monga Iye anali nthawi imeneyo. Ndi kulondola uko? Iye analonjeza zimenezo. Ndipo, kumbukirani, khalidwe Lake ndi chomuzindikiritsa Chake. Ndi angati akumvetsa zimenezo, kwezani dzanja lanu. Khalidwe Lake ndi chizindikiritso Chake.

<sup>141</sup> Monga iwo amene ankachokera ku Emmau, pamene ine ndikunena izi. Yesu anali atapachikidwa. Onse a iwo anali achisoni. Iwo anali mmanda. Tsopano iwo anati, “Winawake anabwera ndipo anadzamuba Iye.” Tsiku lina Iye anatulukira kuchokera mu tchire lina ndipo anayenda limodzi ndi iwo, pamene Iye ankapita ku Emmau. Ndipo iwo anati. . .

Iye anati, “Nchifukwa chiyani inu—ndi chifukwa chiyani inu muli achisoni kwambiri?”

Iye anati, “Chabwino, Iwe ndi mlendo chabe kuno.”

<sup>142</sup> Ndiyeno pamene Iye anawalowetsa iwo mkati, Iye anachita chinachake monga momwe Iye ankachitira asanapachikidwe. Ilo linali khalidwe Lake lochita izo mwanjira imeneyo. Ndipo iwo mwamsanga anazindikira, mwa khalidwe Lake, kuti uyo anali Yesu yemweyo amene anali atapachikidwa. Amen.

<sup>143</sup> Mulungu anamuwukitsa Iye kwa akufa, ndipo lero khalidwe Lake, monga ilo, mofanana monga zinkakhalira nthawi imeneyo! Ndipo kubwerera kwa masiku a Sodomu, monga Yesu analosera, chinthu chomwechonso ndi choti chidzachitike “pamene Mwana akuwululidwa kwa anthu.” Ndi chizindikiritso cha khalidwe Lake. Ahebri 4:14 ndi 15, “Iye tsopano ndi Wansembe wathu Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu,” chimodzimodzi monga momwe Iye ankachitira nthawi imeneyo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Zofooka zathu zimamukhudza Iye. Chabwino, ngati izo zingamukhudze Iye, kodi Iye angachite motani ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Khalidwe lake lingakhale chimodzimodzi. Ndiye Iye angachite monga Iye anachitira pamene mkaziyo anakhudza chovala Chake. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Iye ali moyo nthawizonse, Iye ali moyo nthawizonse, ndipo makhalidwe Ake akumuzindikiritsabe Iye lero monga Iye ankachitira nthawi imeneyo. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo ndi mtima wanu wonse? Mulungu, kuzindikiritsidwa ndi khalidwe Lake, limamuzindikiritsa Iye.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

<sup>144</sup> Atate Akumwamba, ndife amuna ndi akazi chabe amene takhala pano usikuuno. Koma ife tiri, monga zinkakhalira, tikumugwira Mulungu pamene ife tikuwagwira Mawu. Ndipo, Atate, ine ndingachite mantha kuyesera kunena chinachake chimene sichinali muno. Ine ndingachite mantha kuti ndiyesere

kuyika kutanthauzira kwanga kwa Iwo, chifukwa izo zikhoza kukhala zolakwika. Ndipo Inu munati, “Aliyense amene adzachotsa Mawu amodzi kwa Iwo, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Iwo, gawo lake lidzachotsedwa ku Bukhu la Moyo.” Kodi moyo wanga ungakhale wabwino bwanji ndiye, Ambuye, ngati ine ndingachite chinthu choyipa monga chimenecho? Kotero ine ndimangoyankhula Iwo momwe Iwo aliri.

<sup>145</sup> Ndipo, Atate, Inu munalonjeza kuti Inu mudzawazindikiritsa Iwo. Ine ndikukhulupirira kuti Inu munawuka kwa akufa, zaka thuu sauzande zapitazo, ndipo muli moyo usikuuno, kuyitana anthu ophweka basi monga momwe Inu mwakhala mukuchitira nthawizonse, mmodzi *apa* ndi mmodzi *apo*; osati magulu, osati mabungwe, osati machitidwe aakulu a zomwe munthu anachita. Koma Inu munati Inu mudzatenga anthu kuchokera mwa Amitundu, anthu, “Awiri adzakhala mmunda; Ine ndidzamusiya mmodzi, ndikutenga mmodzi. Awiri adzakhala pa bedi; Ine ndidzamusiya mmodzi, ndikutenga mmodzi,” anthu apa ndi apo, kwa Dzina Lanu, Mkwatibwi.

<sup>146</sup> Ine ndikukhulupirira kuti khalidwe Lanu limakuzindikiritsani Inu. Inu munalonjeza, “Monga zinali mmasiku a Sodomu,” chomwechonso izo zidzakhala mu tsiku limene Inu muzidzaululidwa, Mawu. Mawu Iwoeni, a ora lino, akuyenera kuwulula Mawu Iwoeni, monga Mawu anabwerera kwa aneneri. Ndipo, Atate, ife tikumuwona Yohane atayima apa pa dziko lapansi, ndipo apo panali a—Mawu amene iye ankawawulula. Ndipo Baibulo linati, “Mawu nthawizonse amadza kwa mneneri.” Ndipo Mawu anali thupi pamenepo, kotero Iwo anayenda mpaka kukalowa mmadzi, kwa Yohane. Mawu anadza kwa mneneri.

<sup>147</sup> Atate Mulungu, bwerani usikuuno, ine ndikupemphera, ndipo dzatithandizeni ife. Dzathandizeni kusakhulupirira kwathu. Tikhululukireni ife zolakwa zathu. Chiritsani odwala ndi osautsika. Mawu amodzi ochokera kwa Inu, Ambuye, adzatanthauza kuposa chirichonse chimene munthu aliyense angakhoze kunena. Kuyankhula kwanu basi, Atate, Mawu amodzi okha atanthauza mochuluka kwambiri. Tsopano, Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ife tikudzipereka tokha kwa Inu tsopano. Ndipo ife tikupemphera kuti pamene ife tizichoka ndi kupita ku nyumba zathu usikuuno, ife tine monga iwo ankachokera ku Emmau, pamene iwo anamuwona Iye akuchita chinachake kuti azindikiritse kwa iwo kuti Iye anali Ambuye woukitsidwayo. Ziribe kanthu ndi mochuluka bwanji momwe iwo ankati, “Iwo anaba thupi Lake, ndipo—ndipo iwo anachita *ichi*, *icho*, kapena *chinacho*,” iwo anadziwa iwoeni kuti Iye anali ataukitsidwa kwa akufa. Kodi Inu usikuuno simudziwonetsera Nokha wamoyo kwa ife kachiwiri? Ndi kuwayitana iwo mu mzinda wokongola uwu ndi

kozungulira, amene anadzozedweratu ku Moyo, kwa Inu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

<sup>148</sup> Tsopano, ine ndikufunsani inu tsopano kwa pafupifupi maminiti fifitini. Ife tichedwa kwa pafupifupi maminiti teni. Ine ndifulumira. Ine ndikufuna kuyitana makadi apemphero. Ine ndikukhulupirira Billy. . . G, makadi apemphero G, ndi amene iwo anapereka? G, makadi a pemphero G, tiyeni titenge wani mpaka fifitini kapena twente, chinachake. G, wani. Ndi angati. . . Ndani anali ndi G, nambala wani, kwezani mmwamba dzanja lanu, muwone ngati ilo liri pano. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi]. Ndipo, kumbukirani, gwirani makadi anu a pemphero, inu mupempheredwa. Ngati inu simupeza ilo usikuuno, ife tipeza ilo. Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni, eyiti, naini, teni, pomwe apa mwaliwiro momwe mungathere, ndipo muyende mpaka apa pomwe ndi kudzayima mu mzere. Chabwino. Wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni. Atatu akusowa pamenepo. Seveni, seveni, ndi wani, thuu, firii. . . Ndiwerengere iwo, Roy. Chabwino, teni. Chabwino, wani mpaka teni. Fifitini tsopano, G, wani mpaka fifitini, iwo ndi fifi- . . . kapena teni, leveni, thwelovu, sartini, fortini, fifitini. Chabwino. Tiyeni—tiyeni tiyimire pamenepo, awa basi. Chabwino.

<sup>149</sup> Tsopano ife tiri—ife tikuyesetsa kusunga mawu athu, mwaona, kuti tikhale titatuluka pokwana hafu pasti naini, koma ife sitichita izo usikuuno, ine—ine—ine ndikudziwa. Koma tsopano ndikufuna kuti aliyense apereke tcheru chosagawanika.

<sup>150</sup> Tsopano, ngati ine ndayankhula Choonadi ndi kukuuzani inu kuti zinthu izi zikuyenera kuchitika, ndipo ndi izi apa mu Baibulo, kuti ili ndi oralo. Inu mukhoza kukhala kuti munaphunzitsidwa musukulu ina. Ndi momwenso anachitira Afarisi. Koma Baibulo linati, mu tsiku limenelo, “Namwali adzayima,” Iye. . . Iye anatero. Iye anati makhalidwe a Mesiya akanadzakhala *motere*. Iwo anali. Koma iwo sanawakhulupirire Iwo. Izo sizinamulepheretse Iye kumangopitirira chimodzimodzi basi. Chimodzimodzi monga izo zikuchitikira tsopano. Ife tikukhala moyo mmaola otsiriza a tsiku lomaliza.

<sup>151</sup> Sayansi imati kwatsala maminiti atatu kuti tifike pakati pausiku. Ndikuganiza kuti ndi mochedwa kuposera apo tsopano, pafupifupi nthawi iliyonse. Chikominisi chayipitsa dziko, ndipo alaliki atsatura chikominisi mmalo mwa Khristu. Izo zikungowoneka ngati kupita kunja kukayesera kuzitsutsa izo, bwanji osawona ora limene ife tikukhalamo? Chikominisi, ife tiribe. . . Mai, mai! Ine sindikuchita mantha ndi chikominisi. Ndi Kudza kwa Ambuye kumene kudzakugwireni inu musanakonzekere, ndi chimene icho chiri, kwa mpingo. Tsopano lolani aliyense, mulole Amerika yense atembenukire kwa Mulungu, ndipo muwone chimene chidzachitike kwa chikominisi. inu mukuyenera kupeza nthendayo, ndipo kenako nkudzapeza mankhwala ake.

152 Tsopano, aliyense molemekeza, chonde musayendeyende. Tsopano, ndi angati kunja uko amene alibe khadi la pemphero, ndipo inu mukufuna kuti Mulungu akuchizeni inu? Mungokweza dzanja lanu, ndikuti, “Ine—ine—ine—ine ndikukhulupirira.” Ziribe kanthu pamene inu muli.

153 Tsopano penyani, ine ndikuganiza *awa* akugwira ntchito, [M’bale Branham akumenya ndi kuwuzira mu maikrofoni—Mkonzi]. *awa*. Chabwino. Ngati muli ndi...Kodi inu mukundimva kumbuyo kuno? Chabwino. Chabwino. Tsopano inu penyani izo, M’bale Roy.

154 Tsopano, Mawu amodzi ochokera kwa Mulungu atanthauza zochulukira kuposa zonse zomwe ine ndikanakhoza kunena.

155 Tsopano, monga kuyang’ana kuchokera apa, izo ndi zovuta, izi—izi nthawizonse zinali. Mwaona, kuwala kuli pa nkhope yanu pomwe, ndipo zikukhala ngati zovuta kuwona kunja uko kuti ndiwawone anthu.

156 Ndipo ine sindikudziwa. Ine sindikutha kuwona munthu m’modzi, kwenikweni, amene ine ndikukhoza kumuwona tsopano amene ndikumudziwa. Ndi angati a inu amene muli alendo kwa ine, kwezani mmwamba dzanja lanu, mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu. Ndikuganiza kuti ndi paliponse. Ndi angati mu mzere wa pemphero mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu? Kwezani manja anu. Ponse pa mzere wa pemphero pamenepo, ngati inu mukutha kundimva ine, kwezani mmwamba manja anu ngati—ngati ine ndiri mlendo. Aliyense.

157 Tsopano Iye ndi chiyani? Iye ndi Wansembe Wamkulu amene angakhudgidwe ndi kumverera kwa zifooko zathu. Mkazi uja amene anakhudza chovala Chake, iye akhoza kukhala kuti analibe khadi la pemphero, nkomwe, koma iye anamukhudza Iye ndipo, pamene iye anatero, chinachake chinachitika. Tsopano inu mukhudze mwanjira yomweyo, mumukhudze Iye. Ndi angati amene amadziwa kuti Ahebri, mutu wa 4, amati, “Tsopano Iye ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudgidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu”? Ndi angati akudziwa zimenezo? Chabwino, kodi Iye angawonetsere khalidwe Lake lomwelo? Ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, Iye angatero. Chabwino. Tsopano, kodi ichi ndi... .

158 M’bale Pearry, abweretseni iwo kwa ine tsopano. Tsopano ine ndikufuna aliyense akhale molemekeza kwenikweni. Pomwe apa, basi pomwe apa, mlongo.

Tsopano, kodi inu mukundimva ine? Tsopano, ine sindikudziwa. Muyang’ane aliyense amene ali pa—injiniya kumeneko, chifukwa ine sindikudziwa.

159 Masomphenya. Tsopano, kumbukirani, ine si Mesiya, ine si Khristu. Koma Iye ali pano. Icho ndi chimene ine ndikuyesetsa

kuti ndikupangitseni inu kuti muwone, Iye ali pano, Iye akusunga Mawu Ake.

<sup>160</sup> Tsopano, ngati mkazi uyu akudwala, ine sindikudziwa. Ine sindikumudziwa iye. Iye ndi wamkulu kuposa ine. Ife mwinamwake tinabadwa motalikirana zaka, ndi kutalikirana mamailosi, iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukumana.

<sup>161</sup> Tsopano, izi ziri basi monga Ambuye wathu anakumanirana ndi mkazi uja, mu Yohane Woyera 4. Ndikuyesetsa kuti ndizipangitse izo momveka bwino kwambiri kuti musaphonye kuziwona izo, zikatero, pa Malo a Chiweruzo, sipadzakhala magazi mmanja mwanga pa tsiku limenelo. Tsopano, Yesu analonjeza kuti mmasiku otsiriza izi zikanadzachitikanso kachiwiri. Pamene ife tikudutsa msabatayi, inu mupeza. Ilo ndi lonjezo.

<sup>162</sup> Tsopano, ine sindikumudziwa donayu, izi ndi mwamuna ndi mkazi akukumana koyamba. Tsopano, ngati Ambuye Yesu angawulule kwa ine chimene inu mwabwerera kuno, kapena winawake, kapena chimene inu mukuchita, kapena chimene chalakwa ndi inu, kapena chimene inu mwachita, ngati ziri zachuma, zapakhomo, chirichonse chimene chiri, izo zikuyenera kuti zibwere kuchokera ku Mphamvu inayake yauzimu, chifukwa ine sindikukudziwani inu. Ndi angati ati achitire umboni kwa zimenezo, izo zikuyenera kubwera kudzera mu Mphamvu yauzimu? Tsopano, inu mukhoza kusewera ngati Mfarisi, kuvuna kuti ndizo. . . (Kuzungulira mbali inayo, M'bale Roy, mwaona.) Inu mukhoza kusewera ngati Afarisi, ndikuti, “Two ndi mzimu woyipa,” zimene ambiri amachita. Zimenezo ndi za pakati pa inu ndi Mulungu, ndiye. Ndiye inu mukhala ndi mphotho yawo. Koma ngati inu mungati, “Izo ndi za Mulungu,” ndiye inu mudzalandira mphotho Yake. (Tsopano, izo ziri bwino. Zikomo inu.)

<sup>163</sup> Tsopano mungoyang'ana pa ine miniti yokha. Monga Yesu ananena. . . Pamene Petro ndi Yohane ankadutsa pa chipata chotchchedwa Chokongola, anati, “Tayang'ana pa ine.” Ine—ine sindikumudziwani inu. Ndipo tsopano ngati Mzimu Woyera, Winawake pambali pa ine, abwere ndi kudzawulula chimene chiri mu mtima mwanu, ndiye Baibulo linati, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, Lozindikira malingaliro ndi zolinga za mu mtima.” Ndizo ndendende zomwe Baibulo limanena. Tsopano, izo zimawulula ndiye chinsinsi cha mtima. Tsopano, ilo lingakhale khalidwe la Mulungu, Mawu akuwonetseredwa mu tsiku lino. Ndi angati akukhulupirira zimenezo tsopano? Chabwino. Uh-huh. Tsopano inu mukuona chimene icho chiri?

<sup>164</sup> Tsopano ine ndalalikira izo, ndinakuuzani inu za izo, koma kodi izo ndi zoona? Ndicho chinthu chotsatira, mwaona. Tsopano, ngati izo ziri zoona, aliyense wa inu. . . Ngati izo si

zoon, iye adziwa izo. Ndithudi, iye adziwa izo. Inu mudziwa izo, nanunso. Koma ngati izo sizoon, ndiye ine nda—ine—ine ndachitira umboni zolakwika za Khristu. Ngati izo ziri zoon, aliye wa inu apereke mtima wake kwa Iye, mumukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse, ndi kufikirako ndi kumulandira Iye pa chirichonse chimene inu mukuchisowa. Izo zoon.

<sup>165</sup> Tsopano mulole Mzimu Woyera udzizindikiritse Wokha mu Dzina la Yesu Khristu. Tsopano, ine sindikudziwa chimene inu mwabwerera pamenepo. Inu mukungowoneka ngati wowoneka-bwino, mkazi-waumayi mutayima pamenepo, ndipo ndizo zonse zimene ine ndikuzidziwa za inu. Koma Mzimu Woyera ukhoza kuwulula chimene inu mwabwerera pano, chimene chiri vuto lanu, kapena chinachake. Inu mudziwa ngati ziri zoon kapena ayi. Tsopano, ndinu, chimene inu mukufunira pemphero, ndi chinachake chonga akatumba pa nkhope yanu. Ndi mitsempha, monga, pa nkhope yanu. Tsopano, ngati izo ziri zoon, kwezani mmwamba dzanja lanu. Kodi inu mukukhulupirira?

Tsopano, tsopano inu mukhoza kunena kuti, “Iye anangopeka zimenezo.”

<sup>166</sup> Tsopano, iye ndi munthu wabwino. Tsopano, tangoyang’anani apa miniti yokha, mlongo. Ine sindikudziwa chimene Iye anakuuzani inu. Koma chirichonse chimene icho chinali, icho chinali choona. Inu—ndinu mboni ya icho tsopano, sichoncho inu? [Mlongoyo akuti, “Uko nkulondola.”—Mkonzi]. Uko nkulondola. [“Kwa zaka twente.”] Mai! Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu kwa zimenezo? Tsopano, inu mukudziwa kuti Ndi Kukhalapo Kwake, pali Chinachake pano chimene chikukudziwani inu, Chinachake. Monga Yesu ananena kwa mkaziyo, Iye anadziwa pamene vuto lake linali, tsopano Iye wadziwa pamene vuto lanu linali.

<sup>167</sup> Ndipo zikuwoneka ngati kuti mwalemedwa chifukwa cha winawake. Ndi wanu. . . Ndi mwamuna, ndi mwamuna wanu. Iye ali pano, nayenso. Uko nkulondola. Ndipo—ndipo kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuwulula vuto la mwamuna wanu kwa ine? [Mlongoyo akuti, “Inde, ine ndikutero.”—Mkonzi]. Iye ndi bambo wodwalika kwenikweni, ali ndi zovuta. Chinthu chimodzi chimene chikumuvuta iye, ndi vuto la mtima. Iye ali ndi vuto la mtima. Ngati izo ziri zoon, kwezani mmwamba dzanja lanu. [“Uko nkulondola.”] Iye alinso ndi mwela. [“Uko nkulondola.”] Uko nkulondola. Mukuona? Uko nkulondola? Eya. Wamanjenje kwenikweni, eya, wamanjenje kwenikweni. Izo zoon, sichoncho izo? [“Inde.”]

<sup>168</sup> Ngati Yesu ati awulule kwa ine! Iye anamuza Petro chimene iye anali. Ngati Iye ati awulule kwa ine yemwe inu muli, kodi inu mukhulupirira kuti ndi Iyeyo? [Mlongoyo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Sindinu ochokera kuno. [“Ayi.”] Inu mwachokera kummawa kwa kuno, ndinu wochokera ku

Louisiana. [“Kulondola.”] Izo nzoona. Kulondola. Ndipo dzina lanu ndinu Akazi a Coleman. [“Uko nkulondola.”] Bwererani kwanu, Yesu Khristu wakuchiritsani inu. Chikhulupiriro chanu chachita machiritso anu.

<sup>169</sup> Tsopano khulupirirani. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Yesu Khristu akudzizindikiritsa Yekha mu chiwukitsiro Chake! Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsopano, aliyense amene ali ndi malingaliro abwinobwino, akudziwa kuti palibe munthu amene angakhoze kuchita zimenezo.

<sup>170</sup> Tsopano, inu kunja uko, munene kwa Mulungu monga chonchi, “Ine—ine—ine ndikudziwa munthuyo sakundidziwa ine, koteru ine ndipempherera chinachake. Ambuye, kodi ndingakhudze chovala Chanu? Ngati izo ndi choncho, ndiye Inu munazidzindikiritsa Nokha mu chiukitsiro Chanu. Tembenukani, mudirole ine ndikukhudzeni Inu, ndiyeno Inu muyankhule kupyolera mwa iye kwa ine.” Muwone chimene chiti chichitike. Mungoyesera zimenezo.

<sup>171</sup> Muli bwanji, bwana? Kodi mungabwere mbali iyi moyandikira pang’ono? Kuli anthu kumbuyo kwanu uko, mwaona.

<sup>172</sup> Chirichonse tsopano, ndi wanu uliwonse—mzimu uliwonse, uli ngati kugunda. Iwe umawugwira iwo, mwaona, komanso kudziwa malingaliro awo, ndipo izo zimafika, mwaona, iwe umasokonezeka yense.

<sup>173</sup> Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? Kodi inu mukukhulupirira kuti Khristu akhoza kuwulula kwa ine chimene inu mwabwerera pano? Kumbukirani, ife tidzakomana pa Malo a Chiweruzo tsiku lina ndi kudzayankhira pa izi zisikuuno. Inu mukudziwa zimenezo? Vuto lanu, limodzi la iwo, liri ku nsana kwanu. Inu muli ndi mavuto ambiri. Muli ndi vuto la nsana. Ndipo maso anu akupita, muli ndi vuto la diso. Ngati izo ziri zoono, kwezani mmwamba dzanja lanu. Tsopano, inunso mukuchita chinachake chimene mukufuna kuti muchisiye. Kodi izo nzabwinobwino kuti ine ndinene zimenezo? Mukufuna kusiya kusuta kumeneko. Ndipo—ndipo chinthu china, inu mwakhala muli ndi...inu mukumverera kuti icho chakhala chiri chinthu chimene chimakutchingani inu kuti mulandire Mzimu Woyera. Tsopano inu mukufuna kuti mulandire Mzimu Woyera, ndicho chokhumba mu mtima mwanu. Uko nkulondola, gwedezani manja anu monga *chonchi*. Chabwino, izo zakusiyani inu tsopano, pitani, kalandireni Mzimu Woyera, ndipo muchiritsidwe. Mulungu akudalitseni inu, bwana.

<sup>174</sup> Inu mukukhulupirira? Tsopano chonde khalani molemekeza kwenikweni. Tsopano ife tikuchedwa kwenikweni, mungokhala chete mphindi chabe.

175 Inu muli bwanji? Ife ndi alendo kwa wina ndi mzake. [Mlongoyo akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Ambuye Yesu amatidziwa ife tonse. Tsopano musachite mantha, mwaona, inu muli ngati. . . Mwaona, mungokhazikika, ndi Kukhalapo Kwake. Mwaona, ndi zimenezo. Ndi Kukhalapo Kwake. Tsopano inu muli ndi kumverera kwachirendo kwenikweni, kosamvetseka, kokhala ngati kumverera kokoma, kodzichepetsa. Mukuona? Tsopano, kuyima pamaso pa munthu sizingakupangitseni inu kumverera mwanjira imeneyo.

176 Ndi angati anayamba akuwonapo Kuwala kumeneko, Lawi la Kuwala limenelo, Moto? Ilo linajambulidwa komwe kuno mu Texas, nthawi yoyamba, nthawi yachiwiri. Ilo lapachikika pafupi ndi mkaziyo pomwe, mwaona, mu gawo ili tsopano. Ine ndikanakonda inu mukanati. . . ngati inu mukanangowona.

177 Pamene ndinu. . .Siyani kusunthako: ndiicho chimene chimachita zimenezo, mwaona. Mawa usiku ife tidzakhala ndi mzere wa pemphero uwu podzafika naini koloko, mwaona, ine—ine ndikukusungani inu motalikitsa kwambiri. Tiyeni timutenge mkazi mmodzi uyu, ndiye. Miniti yokha.

178 Inu mukukhulupirira, mutakhala pamenepo? Inde, chifukwa cha chofooka chimenecho chimene inu mukuvutika nacho, icho ndi chimene chikukuvutani. Mukuona? Kodi iye anakhudza chiyani? Ine sindikumudziwa mkaziyo. Iye anamukhudza Wansembe Wamkulu. Koma, mwaona, ine ndinatembuzira nsana wanga kwa iye, monga momwe zinachitikira mu nthawi ya Abrahamu. Apa, yang’anani mbali iyi, mlongo, miniti yokha. Inu mukuwoneka kuti muli ndi cholemetsa pa mtima wanu. Icho chiri. Ndi mwana wanu wamkazi kumbuyo uko. Iye ali ndi vuto ndi makutu ake. Uko nkulondola. Inu mukhulupirire tsopano ndi mtima wanu wonse? Chabwino, mungokhulupirira tsopano, ndipo iye akhala bwino.

179 Mukuona chimene ine ndikutanthauza? “Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.” Kodi inu mukukhulupirira?

180 Pali dona wamng’ono amene anatsitsa dzanja lake pansi kumbuyo uko, iye akuyang’ana kumene pa ine. Iye akuvutika ndi matenda a shuga. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza matenda a shuga amenewo, mwakhala pansi apo? Chabwino, inu mukhoza kukhala nacho chimene inu mukuchipempha, ndiye. Mungokhulupirira.

181 Dona apo kuchokera pa inu, ali ndi vuto la thumbo ndi vuto la chikhodzodzo. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa zimenezo, apanga zimenezo kukhala bwino? Chabwino, inu mukhoza kukhala nazo zimene inu mukuzipemphazo. Dzanja la dona wamng’onoyo. Mwaona, tsopano penyani, ingomufunsani iye, Chinachake chokoma

kwenikweni chinamukhudza iye. Mwaona, chikhulupiriro chake, ndi chimene chikuchita izo. Si ineyo. Ndi Mulungu.

<sup>182</sup> Apa, apa pali mwamuna wakhala pomwe pano kumapeto. Iye ali ndi vuto la mapapo, bambo wachikulire uyu wakhala pomwe pano akundiyang'ana ine. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiza izo, bwana? Uyo amene wakhala pafupi ndi inu akuvutika ndi matenda m'thupi mwake. Uko nkulondola, mlongo, gwedezani mpango wanu ngati izo ziri zoono. Chabwino. Chabwino, inu nonse muyike manja pa wina ndi mzake, mukhulupirire ndi mitima yanu yonse. Bambo ndi mwana wamkazi, ndiye bwanji osatero? Ikani manja anu pa wina ndi mzake ndipo mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, Yesu akuchiritsani inu.

Ine—ine ndikutsutsa chikhulupiriro chanu kuti mukhulupirire zimenezo!

<sup>183</sup> Dona wakhala pambuyo pake pamenepo, akuvutika ndi vuto la mmimba. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchizani inu, dona? Limenelo ndi vuto lanu. Ngati izo ziri zolondola, imirirani pa mapazi anu kuti anthu athe kuwona. Mukuona? (Kodi iwo akumukhudza ndani kunja uko?) Nenani, ine sindikulakwitsa, apo pali amayi anu akhala pafupi ndi inu pamenepo. Iwo ali ndi vuto mmatumbo mwawo. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu achiritsa izo, dona? Imirirani, nanunso, ndipo muchiritsidwe.

<sup>184</sup> Mukhulupirire! Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye amadzizindikiritsa Yekha. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake, kapena wantchito? Izo zimawapunthwitsa anthu, kunena “mneneri,” iwo samamvetsetsa.

<sup>185</sup> Tayang'anani apa. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mukuvutika ndi manjenje owonjeza. Inu mukukhulupirira kuti ine ndikhoza kukuuzani inu chimene chinayambitsa izo? Munachita ngozi ya galimoto. [Mlongoyo akuti, “Izo nzoona.”—Mkonzi]. Izo nzoona. Izo nzoona, ngozi ya galimoto, ndipo iyo inavulaza nsana wanu ndipo zinapita kuphewa lanu. Nkulondola uko? Izo zikusiyani inu tsopano. Nthawi ya moyo chabe ndi imene nayonso yavutitsa izo, kuzikokomezwa izo, koma inu mukhala bwino. Pitani, mukakhulupirire ndi mtima wanu wonse. Yesu Khristu akuchizani inu, ngati inu muti mukhulupirire. Amen.

<sup>186</sup> Inu mukukhulupirira? Inu mukukhulupirira kuti Iye akhoza kuchiza nyamakazi? Chabwino, musingopitirira kumayenda ndiye, Iye akuchizani inu.

<sup>187</sup> Ndi angati mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, nenani, “Ine ndikukhulupiriradi ndi mtima wanga wonse”? “Ngati inu mungakhulupirire!”

<sup>188</sup> Inu mukukhulupirira kuti Iye amachiza matenda a shuga ndi kuwapanga anthu kukhala bwino, ali ndi matenda

a shuga, ndi kuwachiritsa iwo? Inu mukukhulupirira zimenezo? Kazipitirirani kumayenda, mukuti, “Ambuye, ine ndikukuthokozani Inu chifukwa cha zimenezo.” Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndipo muchiritsidwa.

<sup>189</sup> Ndi angati mukukhulupirira kunjira uko tsopano, ndi mtima wanu wonse? Musati, mwaona, inu mukuyendayenda, inu mukuwusokoneza Iwo, abwenzi. Ine ndikuuzani inu, ndi angati mukukhulupirira? Mungokweza dzanja lanu, ndikuti, “Ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse.”

<sup>190</sup> Tsopano ndikupemphani inu kuti muchite chinachake. Tsopano, ngati Yesu wasunga Mawu Ake, ndipo akukhulupirira izo, ndipo watsimikizira izo kwa inu, Yesu ananenanso izi, kutuma Kwake kotsirira ku Mpingo Wake, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Tsopano ndi angati mukukhulupirira? Iye anati, “Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Kodi inu mukukhulupirira lonjezo limenelo? Ndiye ikani manja anu pa winawake wapafupi ndi inu.

<sup>191</sup> Ngati Iye sakuchiritsani inu, inu mufa. Inu mwaphimbidwa ndi mthunzi. Koma Yesu Khristu wakuchiritsani inu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Chabwino, ikani anu... kazipitirirani ndipo mukhulupirire tsopano, ndipo inu mukhala bwino.

<sup>192</sup> Bwera, dona. Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu achiza TB ndi matenda a shuga amenewo, akupanga iwe kukhala bwino? Tenga... Chabwino, pita, ukakhulupirire ndi mtima wako wonse, ndipo ukakhala bwino.

<sup>193</sup> Kupemphera, kodi inu mukupemphererana wina ndi mzake? Ikani manja anu pa wina ndi mzake, tiyeni tingopemphera, tonse limodzi. Aliyense ikani manja anu pa wina ndi mzake. Nthawi ikutha. Ikani manja anu pa wina ndi mzake, ndipo tiyeni tipemphere.

<sup>194</sup> Ambuye Yesu, ife ndi otsimikiza kuti Mulungu amadzizindikiritsa Yekha pakati pa anthu Ake. Makhalidwe Ake, monga yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, akudziwonetsera okha. O Ambuye Mulungu, Inu Amene munapanga lonjezo la Mawu, Inu munati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Anthu awa avomereza kuti ndi okhulupirira, okhulupirira mwa Yesu wowukitsidwayo Amene akudzizindikiritsa Yekha tsopano ndi khalidwe Lake lomwelo limene Iye anali pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, kuwapanga Malemba kukhala Choonadi chenicheni, kuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ambuye Yesu, ndi okhulupirira awa ali ndi manja awo pa wina ndi mzake, mu Kukhalapo Kwauzimu kwa wowukitsidwayo, Mwana wa Mulungu wozindikiritsidwa Amene wapangidwa thupi pakati pathu kenanso usikuuno mu thupi la okhulupirira Ake, ine

ndikulamulira mzimu wonyansa uliwonse, kudwala kulikonse ndi nthenda, zichoke kwa anthu awa, pamene okhulupirira awa ali ndi manja awo pa wina ndi mzake. Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole izo zikhale chomwecho.

<sup>195</sup> Nonse amene mutakhulupirire machiritso anu tsopano, amene mukukhulupirira izo pakali pano, mu Kukhalapo kozindikiritsidwa kwa Mwana wa Mulungu wowukitsidwa, amene mukukhulupirira kuti chopempha chanu chapatsidwa kwa inu, ndipo muzindikiritsa chinthu chomwecho, imirirani pa mapazi anu ndi kunena kuti, “Ndikulandira izo ndi mtima wanga wonse.” Imirirani, aliyense, mu Kukhalapo kwa Yesu Khristu, amene muti mukhulupirire. Mulemekezeni Iye! Mpatseni Iye matamando ndi ulemelero. Ingokwezani manja anu mmwamba ndi kumuthokoza Iye. Mulungu atsimikizira lonjezo lirilonse limene Iye anapanga. 🙏

64-0311 Mulungu Amazindikiritsidwa Ndi Makhalidwe Ake  
Municipal Auditorium  
Beaumont, Texas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)